# *Uku Ndi Kutuluka Kwa Dzuwa*

Tiyeni tiweramitse mitu yathu. Ambuye, pamene ife tasonkhana pano mmawa wabwino wa Isitala uwu, kuwona mphukira zazing'ono zikukankhira njira yawo kuti zitulukire, njuchi zikuwulukirapo ndi kumatenga gawo lake, mbalame zikuyimba ngati mitima yawo iphulika ndi chimwemwe, chifukwa pali Isitala. Ife tikukhulupirira kuti Inu munamuwukitsa Yesu kwa akufa, zaka zambiri zapitazo, lero, ndipo ife tikukondwerera tsiku lachikumbutso ili.

2 Ndipo mulole pabwere Isitala pakati pa ife tonse, lero. Mulole ife, monga antchito Ake, tiwamvetse Mawu Ake, kuti ife tinali mu chiyanjano Chake nthawi imeneyo, ndipo kuti tsopano ife tauka ndi Iye ndipo tikukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba.

3 Mudalitse msonkhanowu muno mu kachisi, ndi kudutsa maiko kumene iwo ukupita, mwa lamya iyi.

4 Muchiritse odwala onse ndi osautsika. Mulole iyo ikhale Isitala kwa iwo, nawonso, ndi eksodo kuchoka ku matenda kupita ku mphamvu. Ndipo iwo amene ali akufa mu tchimo ndi kulakwa, mulole iwo akhale amoyo lero kudzera mwa Khristu. Ndipo ife tidzakuyamikani Inu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Ameni.

5 Ine ndithudi ndikuwutenga uwu ngati mwayi wopambana, mmawa uno kuti ndabwerera kuno mu Jeffersonville, Indiana, ndi osonkhana opambana awa, tchalitchi chadzaza ndipo akuimirira, ndi pozungulira ndi kunja, ndi mmalo ndi paliponse. Kwa inu anthu pa mafoni kudutsa fukoli, ndi mmawa wokongola kuno.

6 Faivi koloko mmawa uno, mzanga wamng'ono wa chidali chofiira anawulukira pa zenera ndipo anadzandidzutsa ine. Zimawoneka ngati mtima wake wawung'ono ukanaphulika, akuti, "Iye wauka." Ine nthawizonse ndakhala ndikumalingalira za mbalame yaying'ono iyi za kukhala bwenzi kwa ine, chifukwa ine ndimaikonda iyo.

7 Monga momwe nthano ya iye imanenera, "Mbalame yaying'ono ya burawuni inamuwona Iye akuzunzika pa mtanda, pamene tchimo linamuyikapo Iye." Ndithudi, mbalame yaying'onoyo inalibe tchimo. Iye sankayenera kuti afere mbalame yaing'onoyo. "Koma iyo inawulukira pa mtanda ndipo imayesetsa kuti izule misomaliyo, ndi mlomo wake wawung'ono, ndipo iyo inakhala ndi chifuwa chake chonse chitafiira."

Ndipo umo ndi momwe ine ndikufunira changa, inenso, ngati chishango, choyesera kutetezera Chinthu chaulemelero ichi chimene Iye anachifera.

8 Pozindikira kuti nthawi yathu ndi yoperewera pano, makamaka kwa azimzathu amene akumvetsera pa telefoni iyi, ine ndikufuna ndiyitanire tcheru chanu mmawa uno ku a—chithunzi chimene nthawi yina kalelo chinajambulidwa ndi kamera, cha masomphenya amene ine ndinali nawo kuno ku kachisi, a kuchoka ku Indiana, kupita ku Arizona; kumene ine ndimati ndikakumane nawo, mmawonekedwe a piramidi, Angelo seveni. Ndisakudziwa zomwe zikanati zidzachitike mtsogolo mwake, pamene ine ndidzafike kumeneko, poganiza kuti awo anali mathero a moyo wanga, kuti palibe amene akanapirira kuphulikako; ndipo ndikutsimikiza kuti nonse a inu mukuidziwa nkhaniyo. Ndipo kenako mu Sabino Canyon, mmawa wina monga chonchi, pamene ndinali mu pemphero, panali lupanga limene linayikidwa mdzanja langa, ndipo anati, "Awa ndi Mawu, ndi Lupanga la Mawu."

9 Kenako, Angelowo anadzawonekera monga zinanenedwera. Ndipo pa nthawi yomweyo, kuwundana kwakukulu kwa Kuwala kunachoka kumene ndinali nditayima, ndipo kunasunthira mailosi sarte mmwamba mu mlengalenga, ndi kudzazungulira mkomberowo, monga mapiko a Angelowo, ndipo anadzajambula mu mlengalenga mawonekedwe a piramidi mu kuwundana komweko kwa Angelo amene anawonekera.

10 Sayansi inajambula chithunzi chake, njira yonse kuchokera ku Mexico, pamene icho chinali chikusuntha kuchokera kumpoto kwa Arizona, pamene Mzimu Woyera unati ine ndikanadzakhala nditayima, "mailosi forte kumpoto chakummawa kwa Tucson." Ndipo icho chinapita mu mlengalenga, ndipo *Life* magazine inayika zithunzizo, "Chinachake chachinsinsi mu mlengalenga, kumene sikungakhoze kukhala chinyezi, kumene sikungakhoze kukhala chifunga cha chirichonse; mailosi sarte mmwamba, ndi mailosi twente-seveni chopingasa," ndipo akubwera molunjika kuchokera kumene Angelo awo anali.

11 Tsopano, iwo anandifunsa, kuti adziwe. Sayansi, mmodzi wa iwo ku Tucson, ankafuna kudziwa kufunika kulikonse, koma ine sindinawawuze iwo. Inu nonse mumadziwa izo, munawuzidwa zisanachitike. Koma izo sizinali za iwo; izo zinali za inu.

12 Ndipo chotero pamenepo Iye anayankhula kwa ine, ndipo anati, "Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zidzatsegulidwa. Zinsinsi zisanu ndi ziwiri, chinsinsi chofutukuka pasanu ndi pawiri cha Baibulo, chimene chakhala chotsekedwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, chidzawululidwa." Ndipo ife, komabe gulu laling'ono lodzichepetsa, poyerekeza ndi dziko lapansi lonse, ife tasangalala nawo madalitso awa, kumva zinsinsi

zimenezo. Chikwati, chilekano, mbewu ya serpenti, mafunso onse osiyanasiyana awa, zawululidwa kwathunthu kwa ife, osati ndi munthu, koma ndi Mulungu, Mwiniwake, amene watsegula zinsinsi zisanu ndi ziwiri zimenezo; za chimene Mpingo unali, momwe Iwo unali mwa Khristu pachiyambi, ndi momwe Iwo ukanati udzawululidwe mu tsiku lotsiriza.

13 Ndipo tsopano, pamene ichi chimakwera mmwamba, ife tiri nacho chithunzicho panja pa chokorekapo icho. Koma, ndiye, ine ndiri nacho chithunzicho pano, ngati inu mungazindikire, monga momwe *Life* magazini inali nacho icho. Koma ine ndikudabwa ngati omvetsera anga, owoneka pano, anayamba ayang'anapo kwenikweni pa chithunzicho, mwawona, mwawona, momwe chiyenera kukhalira.

14 Inu mukukumbukira, ndinali ndikulalikira pamene masomphenya awa anabwera, pa phunziro la Bukhu la Chivumbulutso, kumene oweruza akale, kumene ife tinamuwona Yesu mu Chivumbulutso 1. Pamene ife tinayamba kutsegula Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. . . kapena—kapena Mibadwo ya Mpingo, kani, basi pambuyo pa kutsegulidwa kwa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Khristu anali atayima ndi "tsitsi ngati ubweya, woyera." Ndipo ndinafotokoza izo kwa inu, kuti oweruza akale Achingerezi, ndi oweruza akalekale, pamene iwo akupita poweruzira, kuti akalumbiritsidwe, ulamuliro wawo wapamwamba unkapatsidwa kwa iwo. Iwo ankavala wigi yoyera, monga momwe zinkakhalira, pamwamba pa mitu yawo, kuti awonetsere ulamuliro wawo wapamwamba.

15 Chabwino, ngati mungachitembenuze chithunzicho monga *chonchi* ndi kuyang'ana, mukhoza mwinamwake kuchiwona icho kuchokera kwa omvetsera, ndi Khristu. Mwawawona maso Ake akuyang'ana *apa,* mwangwiro basi monga izo zingakhoze kukhalira; atavala wigi yoyera ya Umulungu Wapamwamba ndi Woweruza wa miyamba yonse ndi dziko lapansi. Kodi inu mukutha kuwawona maso Ake, mphuno, kamwa Yake? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mungochitembenuza chithunzicho kuchokera kwa *ichi,* momwe iwo anajambulira icho; mbali *iyi,* momwe icho chiyenera kukhalira. Ndipo inu. . . Kodi inu mukukhoza kuchiwona icho? ["Ameni."] Iye ndi Woweruza Wamkulu. Palibe wina koma Iye. Ndipo icho ndi chizindikiritso changwiro kachiwiri, chitsimikizo kuti Uthenga uwu ndi Choonadi. Ichi ndi Choonadi. Ndi zoona. Ndipo kumupanga Iye osati Munthu wachitatu, koma Munthu yekhayo!

16 Ndi yoyerayo mukuona, inu mukuona kudako, nkhope Yake, ndevu Zake, ndi maso Ake. Ndipo zindikirani, Iye akuyang'ana. . . Kuchokera kwa Iye kukubwera Kuwala uku kukuwalira ku mbali ya dzanja lamanja, kumene Iye akuyang'anako. Ndipo pa mtanda, ndi pamene Iye anayang'ana, kumanja, kumene Iye anamukhululukira wochimwa. Mu

Kuwala kwa chiwukitsiro Chake, ife tikupitabe chitsogolo mu Dzina Lake.

17 Ine ndikukhumba, mmawa uno, kuti ine ndikanakhala ndi nthawi yochuluka basi yo—kuti ndiyigwiritse ntchito pa zochitika izi zimene kudutsa mthunzi uliwonse wa kukayikira, zatsimikiziridwa kwa zaka sarte zapitazi, kapena zaka sarte-faivi, pomwe pano pa mpingo uno; kuyambira uko pa mtsinje, pamene Kuwala komweko kunabwera cha kuno ku Jeffersonville, mu 1933, ndipo kunadzayankhula mawu amenewo, "Monga Yohane M'batizi anatumidwa kuti adzatsogolere kudza koyamba kwa Khristu, Uthenga wako udzatsogolera kwachiwiri." Ife tiri ku nthawi yotsiriza, ndipo ife tikuziwona izo. Ife timadabwa nthawizina chifukwa chimene izo sizinafalikire padziko lapansi; mwinamwake nthawiyina tidzakhala ndi mwayi woti tifotokoze izo, ngati Mulungu alola.

18 Tsopano ndikufuna kuti inu mutembenuzire mu—mu Mabaibulo anu, monga ife nthawizonse timakhulupirira kuti Mawu ayenera kubwera poyamba, kuwerenga kwa Mawu. Ine nthawizonse ndimawerenga Iwo, chifukwa Iwo . . . Mawu anga ndi mawu a munthu, iwo adzalephera; koma Mawu a Mulungu sangalephere konse.

19 Tsopano ti—tiwerenga kuchokera mu Malemba Oyera, mutu. Ndipo ife tikufuna kuti inu mutembenuzire, poyamba, ku malo atatu mu Baibulo, amene ine ndawasankha kuti ndiwerengeko. Amodzi a iwo ali mu Chivumbulutso, mutu wa 1, ndipo ndime ya 17 ndi ya 18; apa ndi pamene Iye anawonekera ali ndi "Tsitsi Lake loyera ngati ubweya; ndipo mapazi ake anali ngati mkuwa." Ndipo kenako ine ndikufuna kuti inu mupeze, mu Mabaibulo anu, Aroma 8:11. Ine ndasankha, mmawa uno, malo atatu oti ndiwerenge, kuchokera mu Malemba Oyera, kwa Uthenga wanga lero, umene Ambuye wayika pa mtima panga wa chiwukitsiro. Ndipo kenako ine ndikufuna kuti inu, aponso, Marko 16:1 ndi 2. Pamenepo ine nditengapo yanga—nkhani yanga.

20 Tsopano mu Chivumbulutso 1:18, ife tikuwerenga Mawu awa, 17 ndi 18.

> *Ndipo pamene ndinamuwona iye, ine ndinagwa pa mapazi ake ngati wakufa. Ndipo anayika dzanja lake lamanja pa ine, ndikunena kwa ine, Usawope ayi;* pakuti Ine *ndine woyamba ndi wotsiriza:*
>
> *Ine ndi iye amene ali wamoyo, ndipo ndinali wakufa; ndipo, taonani, Ine ndiri wamoyo kwa nthawizonse, Ameni; ndipo ndiri ndi mafungulo a* imfa ndi gehena.

21 Ndipo mu Aroma mutu wa 8 ndi ndime ya 11, ife timawerenga izi.

> *Koma ngati Mzimu wa iye amene anamuwukitsa Yesu kuchokera kwa akufa udzakhala mwa inu, iye*

*amene anamuwukitsa Khristu kwa akufa nayenso adzafulumizitsanso matupi anu achivundi ndi Mzimu wake umene ukukhala mwa inu.*

22 Ndipo tsopano mu Marko mutu wa 16, mutu wa chiwukitsiro, mutu wa 16, ndime ya 1 ndi ya 2.

*Ndipo pamene sabata linapita, Mariya Magadala,* amake. . .*ndi Mariya amake a Yakobo, ndi Salome, anali* atabweretsa *zonunkhira zokoma, kuti abwere kudzamudzoza iye.*

*Ndipo molawirira kwambiri mmawa tsiku loyamba la sabata, iwo anabwera kumanda pa kutuluka kwa dzuwa.*

23 Tsopano, mutu wanga mmawa uno, ine ndikufuna kuti nditenge ngati mutu: *Uku Ndi Kutuluka Kwa Dzuwa.* Ndipo kwa phunziro, ndikufuna kuti ndigwiritse ntchito, "Mphamvu yofulumizitsa."

24 Tsopano, inu mukudziwa, inu mwinamwake mwakhala mukumvetsera wailesi ndi atumiki osiyanasiyana akuyankhula. Ndiponso wathu M'bale Neville wochirimika mmawa uno amayankhula phunziro lake la Isitala, pa chiwukitsiro. Ndipo ine ndinaganiza mwinamwake nditenge a—njira yosiyana pang'ono, osati kuti ndikhale wosiyana, koma kungoti ndiwonjezere pang'ono, mwinamwake mu ngodya ina, kwa inu. Malemba, ngodya iliyonse imene inu mungapite ndi Malemba, Iwo nthawizonse amamufotokoza Yesu Khristu. Inu simungachokeko kwa izo, mulimonse. Iwo nthawizonse amamulengeza Iye.

25 Tsopano, monga dziko lero mu a—msonkhano wachikumbutso, kapena, pafupifupi, mu United States ndi mbali ino ya dziko lapansi, mmawa uno, mmipingo ndi konsekonse, akukondwerera chikumbutso cha—cha chigonjetso chachikulu chimene munthu anayamba wakhalapo nacho.

26 Ine ndikuganiza, ngati Mpulumutsi pamene Iye ankafa, kapena ngati khanda pamene Iye anabadwa, Iye sakanakhala pano popanda kubwera padziko lapansi. Ndipo pamene Iye anafa, ndithudi Iye anatetezera tchimo lathu. Koma, komabe, pakhala pali ana aang'ono abwino amene abadwapo, ndipo pakhala pali anthu ambiri amene anazunzika ndi kufa pa chifukwa chenicheni, koma panali pasanakhalepo mmodzi amene akanatha kudziwukitsa yekha kachiwiri kufikira tsiku ili.

27 Tsopano, kuti ili ndi sabata lalikulu kwambiri mu mbiriyakale, chikondwerero chachikulu kwambiri cha nthawi zonse, Isitala iyi ndi pamene Iye anatsimikizira chimene Iye ananena. Munthu akhoza kunena zinthu, komabe izo siziri ndendende zomwe zingakhoze kukhulupiririridwa, bwinobwino, mpaka izo zitatsimikiziridwa kuti ndi Choonadi.

Ndipo monga Mulungu, Yemwe anati, "Tsimikizirani zinthu zonse; gwiritsitsani kwa icho chimene chiri chabwino," Iye sakanakuwuzani inu kuti muchite chinachake chimene Iye sakanadzachichita Iyemwini. Chotero Iye anatsimikizira Yemwe uyu anali amene anafera tchimo lathu.

28 Ndipo, tsopano, si tsiku lachikumbutso lokha, la maluwa opambana awa a Isitala, ndi zipewa za Isitara, ndi akalulu apinki, ndi zina zotero, zomwe ife talowamo, ndi chikondwerero choyera; zomwe ndi zabwino, koma ichi si chinthu chenichenicho mwa njira imeneyo.

29 Monga momwe anthu lero akuyesetsera kumati, "Ife tiyenera tizisambitsana mapazi kamodzi pa chaka, la—Lachinayi, ndipo Lachisanu tiyenera tizidya mgonero," ndi ziphunzitso zonse zosiyanasiyana za. . .Iwo amatsutsana kuti kodi liyenera lizikhala tsiku *ili* kapena tsiku *ilo*, kapena kodi liyenera lizikhala tsiku la sabata kapena tsiku loyamba la sabata; kapena. . .Zinthu zonsezi ndi mwambo chabe basi. Nchabwino chanji chimene chirichonse cha zimenezo chingakuchitireni inu, kaya inu munali ndi Lenti kapena simunakhale ndi Lenti, ngati mulibemo Moyo mwa inu? Ndi chikumbutso chabe. Chimene, palibe chinthu chotsutsana nazo, koma iwo ndithu achita miyambo yawo, koma achisiya chinthu chenichenicho.

30 Satana samasamala momwe inu muliri wachipembedzo, kapena momwe muliri wolondola mu Chiphunzitso chanucho. Ngati inu muwuphonya Moyo umenewo, inu simudzadzukapo, mulimonse. Ziribe kanthu ndinu wachipembedzo bwanji, wabwino bwanji, ndi mipingo ingati imene mwakhalamo kapena mudzakhalamo, zimenezo ziribe kanthu kamodzi pokhapokha ngati mutabadwa mwatsopano.

31 Chotero, ngati Mulungu anamuwukitsa Yesu kwa akufa, kodi Iye anamuwukitsira Iye ngati chikumbutso? Ndipo kodi mmawa wa chiwukitsiro uwu ndi—tsiku limodzi mu chaka, kapena tsiku linalake limene timakondwerera izi? Kapena, kodi ndife opindula a chiwukitsiro Chake? Kodi zimatanthauza chiyani kwa ine? Kodi zimatanthauza chiyani kwa inu? Tsopano ife timakhulupirira, mwa chikhulupiriro, kuti Iye anauka kwa akufa, koma kodi zimenezo ziri ndi chochita chanji ndi ine? Zimenezo zinali zaka zikwi ziwiri zapitazo.

Tsopano kuti ndiwupeze mutu uwu!

32 Pamene ndinali nditatopa, nkono wanga umandipweteka, chifukwa cha katemera amene namwino anandipatsa. Chifukwa, ndikupita kutsidya kwa nyanja tsopano, monga inu mukudziwira, mmasiku ochepa, ndipo ine ndimayenera kubaitsa katemera uyu, mwana wanga ndi ine. Ndipo ndi kolera, yellow fever, ndi chirichonse, ine ndinali wotopa kwambiri, zinandipangitsa ine kudwala. Chimene, Kaisara amafuna kuti ukhale ndi akatemera awa iwe usanapite ku

fuko lina. Ndipo Iye anati, “Perekani kwa Kaisara zimene ziri za Kaisara, komanso mupereke kwa Mulungu zimene ziri za Mulungu.”

33 Ndipo pamene ine ndinali nditakhala pamenepo, ndikudabwa kuti ndikayankhula chiyani kwa omvetsera amene akuyembekezera mmawa uno; chimene ine ndikuthokoza kwambiri, ndipo amuna ndi akazi amene angayike moyo wawo pa chingwe pa zomwe iwe ungayankhule. “Kodi ine ndizichita motani izo? Kodi nditenge chiyani ngati mutu?”

34 Ndipo kenako pamene ine ndinali nditakhala pamenepo, pafupifupi nditagona, chitseko changa chinadzapanga phokoso, kuchokera ku mbali yakutsogolo kwa nyumbayo. Pokhala kuti kunalibeko aliyense koma ine ndekha, monga momwe ndimadziwira. Ine ndinadzamvetsera. Ine sindinazimvetse izo bwino. Patapita kanthawi, chitseko cha chipinda cha kowerengera, kumene ine ndimakawerengerako, chinadzaphokosera, ndipo winawake anali akungogwedeza chitsekocho. Ndipo ine—ine ndinadzapita pachitsekocho ndipo ndinadzatsegula chitsekocho, ndipo, mwakudabwitsidwa kwanga, a—mtsikana, wokongola, wamng’ono watsitsi-lachikasu, wamaso a buluu anayima pamenepo, amawoneka ngati duwa laling’ono la Isitara; amene wakhala apa akundiyang’ana ine tsopano.

35 Anadzandipatsa ine khadi. Ndipo iyo inali . . . Ndithudi, ine ndikuganiza ine ndikafika kunyumba kukakhala makadi a Isitara, ndi zina zotero; koma imodzi yokhayo, pamene ndimanyamuka kunyumba, imene ndinali nditalandira. Ndipo iye anati, “M’bale Branham, iyi ikuchokera kwa adadi ndi ine.” Iye amafuna kuti atsimikize kuti “ine” anali mmenemo. Ndipo abambo ake a nyamakazi, akhala mu chikuku, anali atatumiza khadi iyi. Pamene ine ndinaitenga iyo ndi kumuthokoza wokondedwa wamng’onoyo, pamene iye amatembenuka ndi kuchoka pakhomopo, ine ndinadzaitsegula khadiyo.

36 Ndipo mmawonekedwe a khadi iyi ine ndinatengapo mutu wanga. Pakuti, pa khadiyo panali Marko Woyera 16:1 ndi 2, kutuluka kwa dzuwa, dzuwa linali likutuluka. Kenako ine ndinadzaganiza za zimenezo, ndipo kenako mutu wa “kufulumizitsa,” za Yesu Khristu kuti anawukitsidwa kwa akufa, ndinatengapo phunziro langa.

37 Tsopano, dzuwa, pa kutuluka kwa dzuwa. Chabwino, inalipo nthawi imene dziko linali mumdima wandiweyani. Ilo linali lopanda mawonekedwe, ndipo linali lopanda kanthu. Ndipo ilo lonse linali litakutidwa ndi madzi, ndipo linali pamenepo mu chikhalidwe cha mdima, cha chimbuuzi, cha kulunda. Ndipo Mzimu wa Mulungu unkayenda pa madzipo, ndipo anati, “Pakhale kuwala.” Mulungu anali ndi chifukwa chimene amachitira zimenezo, pakuti pansi pa madzi amenewo panali

mbewu zimene Iye anali atazibzala, ndipo izo zinkayenera kuti zikhale ndi kuwala kwa dzuwa kumeneko kuti kupangitse izo zikhale ndi moyo.

38 Ndipo Kuwala koyamba kumene kunaperekedwa konse pa dziko lapansi kunali Mawu olankhulidwa a Mulungu. Kuwala koyamba kumene kunakhudza konse dziko lapansi kunali Mawu oyankhulidwa a Mulungu. Iye anati, "Pakhale kuwala," ndipo panali kuwala. Zimenezo zinasintha mdima kukhala kuwala, ndicholinga chakuti zibweretse chirengedwe cha chimwemwe ndi moyo padziko lapansi. Kenako, Mzimu wa Mulungu, pamene Iwo unkayenda ndi chikondi ndi chifundo, pa tsiku lalikulu limenelo, tsiku loyamba la kutulukira kwa chirengedwe pa dziko lapansi; dzuwa linatuluka ndipo linadzasesa paliponse, kuwala kwake, ndipo linadzawumitsa madzi pa dziko lapansi, ndipo linadzapanga thambo pamwamba. Ndipo, kwa nthawi yake yoyamba, ilo linali loti libweretse chimwemwe ndi moyo pa dziko lapansi, mwa mbewu. Limenelo linali ora lalikulu.

39 Koma, oh, iko sikunali kanthu, kutuluka kwa dzuwa kumeneko, monga kutuluka kwa dzuwa mmawa wa Isitala ija. Nthawi iyi, ndi dzuwa likulumphira mu mlengalenga, zinabweretsa kutuluka kwa dzuwa kwakukulu kuposa kale lonse; chifukwa kunabwera nkhani yopambana ndi kutuluka kwa dzuwa uku, kuposa momwe zinachitikira ndi kutuluka kwa dzuwa kwa pachiyambi. Kutuluka kwa dzuwa uku kunabweretsa nkhani, yakuti, "Iye wauka! Iye wafulumizitsidwa kwa akufa, monga Iye analonjezera. Iye wauka kwa akufa."

40 Nthawi yoyamba imene dzuwa linadzatuluka, mu Genesis, ilo linali likubweretsa uthenga wakuti padzakhala moyo pa dziko lapansi, moyo wachivundi.

41 Koma nthawi iyi, pamene dzuwa linkatuluka, panali a— kutuluka kwa dzuwa kwapawiri; lina, Mwana, akuwuka. Iko kunali . . . osati d-z-u-w-a lokha likutuluka, anali M-w-a-n-a amene anali atawuka kuti adzabweretse Moyo Wamuyaya kwa Mbewu yonse yolonjezedwa ya Mulungu imene mwa kudziwidwiratu Iye anali atayiwona ili pa dziko lapansi.

42 Sizikanathekanso kuti—moyo wa zomera ukhale moyo kumbuyoko pachiyambi popanda d-z-u-w-a kuti libweretse izo ku moyo; osatinso kuposa, lero, pamene ana a Mulungu ali pa dziko lapansi, zitengera Kuwala kwa M-w-a-n-a kuti kuwabweretse iwo ku Moyo Wamuyaya, Osankhidwa Ake amene Iye anawadziwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Iye anali atawasankha iwo mwa Iyemwini maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

43 Ndipo mmawa wa Isitala, ndiye, mu dothi ili kwinakwake munali matupi athu pa nthawi imeneyo, pakuti ndife fumbi la dziko lapansi. Ndipo Kumwamba, kunali Bukhu

la chikumbutso, ndipo zikhumbo Zake zinali mwa Iye, podziwa kuti chifukwa Mwana uyu wa Mulungu anawuka, Iko kudzawukitsanso ku Moyo mwana aliyense amene anadziwidwiratu ku nthawi yayikulu iyi. Iye ankadziwa kuti izo zikanadzachitika. Ndipo kunali kutuluka kwa dzuwa kwaulemerero bwanji kuposa mmene zinakhalira pachiyambi, panthawi imene kunacha koyamba!

Tsopano, pa kumatula kwakukulu uku kwa Chisindikizo cha Isitala!

44 Tsopano, lero ife tiri ndi chifuwa chachikulu, chisindikizo cha Isitala. Anthu amatumizirana uthenga, wina kwa mzake, ndi kuthandizira thumba lalikulu ili kapena kuyendetsa, la madokotala ndi sayansi ya zamankhwala kuti agwire ntchito pa chinachake, kuti achepetse kapena kuthandizira chifuwa chachikulu. Izo ndi chisindikizo, chimene ife timachitcha chisindikizo cha Isitala, pamene ife titumizirana uthenga kwa wina ndi mzake. Koma pamene ife tilandira uthengawo, chisindikizo chimenecho chimatulidwa, chifukwa chisindikizo ndi chimene chimakhala ndi uthenga utamangidwa mkatimo.

45 Ndipo tsopano, Chisindikizo choona cha Isitala, pa kutuluka kwa dzuwa uku, chinamatulidwa; ndipo chinsinsi cha Moyo pambuyo pa imfa chinawululidwa. Nthawi imeneyo isanafike, ife sitinkadziwa. Dziko lapansi linasonkhana mu mdima, linkapapasa pozungulira, kukayikira kwa munthu. Malingaliro anali pakati pa mtima wa munthu, miyambo yopangidwa. Anthu ankapembeza mafano. Iwo ankapembeza dzuwa. Iwo ankapembeza milungu ya mitundu yonse. Ndipo mitundu yonse ya anthu amene ankadzinenera, iwo onse analowa mmanda, ndipo iwo anakhala mmandamo.

46 Koma Chisindikizo chenicheni chinali chitamatulidwa, ndipo Mmodzi Yemwe nthawi yina anakhalapo moyo monga ife timakhala moyo, anafa monga ife tidzafa, anawukitsidwa kwa akufa. Ndi mmawa wotani! Sunakhalepo umodzi ngati iwo, mu mbiriyakale yonse ya mdziko. Chinsinsi chinadziwika kuti Iye anali ziwiri zonse chiwukitsiro ndi Moyo.

47 Ndipo Iye anati, pamene Iye anadzatulukira mmawa umenewo, "Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo." Sikuti ndi Iye yekha amene anali wopindula wa chiwukitsirocho, koma Mbewu yonseyo imene inali ikupumula mu lonjezo lalikulu la Mulungu inali yopindula ya chiwukitsiro cha ku Moyo chimenecho. Chifukwa, Iye anati, "Chifukwa Ine ndiri ndi moyo, inunso mudzakhala moyo." Kumeneko kunali kumatula kwa Chisindikizocho. Chifukwa Iye anadzutsidwa, chomwechonso aliyense amene ali mwa Khristu adzadzutsidwa limodzi ndi Iye.

48 Pa kutuluka kwa dzuwa kwaulemelero uku, Mulungu anali atatsimikizira, kapena kuwatsimikizira, Mawu Ake. Kulunda

konse ndi kukayikira kumene kunali kutasunthira mmalingaliro a anthu kunali kutachotsedwa, chifukwa apa panali Iye Amene anakhalapo moyo nthawi yina, ankadya, ankamwa, ndi kumayanjana ndi anthu, amene anati, "Ndiri ndi mphamvu ya kuwutaya moyo Wanga; Ine ndiri ndi mphamvu ya kuwukitsa iwo kachiwiri." Ndipo tsopano osati kokha kuti Iye anangonena nenolo, koma Iye anatsimikizira izo kuti zinali Choonadi. Oh, ndi chinthu chaulemelero bwanji chimene icho chiri!

49 Ine ndikutsimikiza mmawa uno kuti ngakhale ife, amene timakhulupirira zimenezo, sitingathe kumvetsa chinthu chachikulu chomwe icho chinali. Chifukwa Iye anawuka kwa akufa, nafenso tawuka kale kwa akufa, pakuti ife tinali mwa Iye.

50 Zindikirani tsopano. Monga kulunda kunaphimba dziko lapansi, ndipo mbewuzo sizikanakhala moyo popanda d-z-u-w-a kuti lituluke, ndipo kulunda kunali kutaphimba dziko lapansi. Ndipo tsopano M-w-a-n-a anawuka, ndipo kulunda konseko kunasowapo ndi Kuwala uku, pamene Iko kunkafalikira kudutsa mafuko, kupita kwa anthu, kuti, "Iye sali pano, koma Iye wauka!" Ndi a—neno bwanji! Iye anali atatsimikizira Mawu Ake. Iye anali atatsimikizira Iwo, kuti anali owona, pakuti tsopano Iye anali atagonjetsa imfa, gehena, ndi manda.

51 Utatu wa mdierekezi: imfa, gehena, ndi manda; pakuti Satana ndi woyambitsa wa imfa, iye ndi mwini wa gehena, ndiponso manda. Ndipo umenewo unali utatu wa Satana, ukuyambitsidwa ndi chinthu chimodzi, icho chinali imfa. Imfa, iwe umapita kumanda; ndipo pokhala wochimwa, umapita ku gehena. Zonsezo chinthu chimodzi chomwecho, utatu wa Satana, imene inali imfa. Izo zinali zitamugwira munthu mu ukapolo zaka zonsezi.

52 Koma tsopano utatu woona wa Mulungu, pokhala Mmodzi woonetseredwa mwa Khristu, Amene anali Moyo, ndipo anamatula Zisindikizo ndi kumugonjetsa mdani, ndipo anawuka, Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo. "Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo wamoyo kwa nthawizonse, ndipo ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade." Mulungu, mwa Mmodzi, anamupanga Munthu, ndipo anadzakhala pakati pathu, ndipo anamgonjetsa mdani aliyense. Ndipo anali atatsimikizira kuti utatu wa Satana unagonjetsedwa, ndi kuti utatu wa Mulungu unadziwika, chifukwa Mulungu yekha anali ndi mphamvu yobwezeretsa Moyo kachiwiri. Iye anali Emanuele uja. Mulungu anali atawonetseredwa mu thupi.

53 Nzosadabwitsa Iye anakhoza kudzinenera pamenepo, Mateyu mutu wa 27, "Mphamvu zonse Kumwamba ndi dziko lapansi zaperekedwa mdzanja Langa. Ine ndikutumizani inu kuti mukakhale mboni Zanga, ku dziko lonse lapansi." Iye anali atagonjetsa zonse imfa, gehena, ndi manda. Osati kokha

kuti Iye anachita zimenezo; ndi kutuluka, mwachipambano, ndi mphamvu zonse Mmiyamba ndi pa dziko lapansi. Zonse zimene zinali Atate, zonse zimene zinali Mzimu Woyera, ndi zonse zimene zinakhalapo, zinali mwa Iye. "Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zapatsidwa kwa Ine." China chirichonse ndi chopanda mphamvu. Iye anali atagonjetsa izo.

54 Tsopano! Ndiyeno, osati zokhazo, Iye anatumiza Mawu kwa ophunzira Ake, okhulupirira Ake. "Musawope, pakuti Ine ndi Iye amene ndinali wakufa, ndipo ndiri wamoyo kwa nthawizonse. Ndipo ndiri nawo mafungulo a imfa ndi gehena; Ine ndagonjetsa kale zimenezo. Musawope panonso, pakuti Mbewu ya Mulungu iliyonse yodzozedweratu, yokonzedweratu idzabwera ku Moyo pamene Kuwala kumeneko kudzafalikira pa dziko lonse, kwa Uthenga waulemelero. Mu m'badwo uliwonse, Iko kudzabweretsa mbewu imene Mulungu anaidzoza Iko kuti kudzachite." Iye anali atauka kwa akufa.

55 Oh, ndi chinthu chodabwitsa bwanji ichi, "Ndine wamoyo, kapena ndafulumizitsidwa." Mawuwo amatanthauza, mawu akuti *kufulumizitsidwa,* mawu Achigriki amatanthauza kuti icho ndi chinachake chimene chapangidwa "kukhala moyo pambuyo pa imfa."

56 Monga—mbewu imene imalowa mu nthaka, iyo imayenera kuti ife, chidutswa chirichonse cha mbewuyo. Iyo imayenera kuvunda, chidutswa chirichonse cha mbewuyo. Ndipo chidutswa chirichonse cha moyo, umene unali mu mbewuyo, chimayenera kuphukiranso.

57 Iye anali "atafulumizitsidwa." Osati zokhazo. "Ndipo ndidzatumiza Moyo womwewo umene unandifulumizitsa Ine, Mphamvu imene inanditulutsa Ine kuchokera mmanda, Ine ndidzatumiza Iwo pa inu, kuti udzakufulumizitseni inu, kuti kumene Ine ndiri kumeneko inunso mudzakakhalenso."

58 Mu Luka, mutu wa 24, ndime ya 49. Iye anati, "Taonani, Ine nditumiza lonjezo la Atate pa inu; koma dikirani, kapena yembekezerani, mu mzinda wa Yerusalemu, mpaka inu mutadzavekedwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba." Kuti akasonyezere kuti Iye sanangotenga zopindula zonse kuchokera mmenemo, koma Iye anagawa zomwe anapindulazo.

59 Iye anabwera kuti adzawombole, kapena kuti adzabweretse ku Moyo, Mbewu zokonzedweratu izo zimene Mulungu anaziwona maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe ndipo anaika maina awo mu Bukhu la Moyo. Ndipo apa iwo ali padziko lapansi, opanda chiyembekezo; Iye anabwera osati kokha kuti adzakhale Mdalitso, koma kuti adzagawane Mdalitso ndi Mbewu iliyonse yokonzedweratu. Tsopano, ngati Mbewuyo ikanati isakhale pa dziko lapansi, Iyo sikanakhala moyo. Iyo inkayenera kuti ikhale pa dziko lapansi, ndiponso kumera. Ziribe kanthu ndi motalika bwanji momwe Iyo yasungidwira

mu mdima, Iyo idzaphukira pamene M-w-a-n-a adzawalira pa Iyo. Zindikirani tsopano, Iye anabwera kudzagawana Iwo ndi ife.

60 Nzosadabwitsa kuti Uthenga ndi nkhani yabwino. Mawu omwewo akuti *Uthenga* amatanthauza "nkhani yabwino." Nkhani yabwino, chiyani? Ngati munthu anafa chifukwa cha ife, imeneyo ndi nkhani yabwino. Ngati Khristu anabadwa, imeneyo ndi nkhani yabwino. Koma sipanakhalepo nkhani, sipanakhalepo nkhani ngati nkhani iyi, kuti, Iye Amene anapanga lonjezo watsimikizira lonjezolo, kuti, "Iye ndi wamoyo kwa nthawizonse, ndipo ali nawo mafungulo a imfa ndi hade, mdzanja Lake." Kulunda konse kunasasidwapo. Panalibenso kulunda koti kuwoneke, pakuti Mwanayo anali atatuluka mmanda. Kunalibeko zakuti, "Chabwino, Iye adzabwera, kapena Iye akhoza kusabwera." Iye anali atabwera kale, Uthenga, nkhani yabwino!

61 Zindikirani, Uthenga womwewo wa Nkhani yabwino, Pawokha, ndi woti ukatsimikizire kwa anthu kuti Iye wauka. "Pitani mukawauze ophunzira Anga kuti Ine ndawuka kwa akufa, ndipo Ine ndikakomana nawo, kuti ndikatsimikizire izi kwa iwo." O Mulungu, momwe mu tsiku lotsiriza lino kudzakhala Kuwala kenanso kudutsa pa dziko lapansi! "Ndipo Ine ndikatsimikizira kwa ophunzira Anga! Pitani mukawauze iwo kuti Ine sindine wakufa, ndipo Ine si mwambo, koma Ndine Khristu wamoyo. Ndikakomana nawo iwo. Mutengere Uthenga uwu kwa ophunzira Anga, kuti Ine ndawuka kwa akufa," Uthenga, nkhani yabwino.

Inu mukuti, "Nkulondola uko?"

62 Ahebri 13:8 anati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ife, opindula Ake, ndi woti titsimikizire kuti Moyo Wake uli mwa ife tsopano, opindula a Moyo uno. Moyo, sipanayambe pakhalapo moyo umene unakhalidwa wonga umenewo; Iye anali Mwana wa Mulungu. Ndipo Iye anafa, ndipo izo zinatsekereza izo; koma pamene Iye anawukanso kwa akufa, mmawa wa Isitala, ndiye ife, monga antchito Ake, tinatumidwa ndi Iye kuti tipite ku dziko lonse lapansi ndi kuti tikafikitse uthenga uwu kwa munthu aliyense, kuti Iye ndi wamoyo. Ndipo ife tingachite bwanji izo mwa Mawu okha? Pakuti kunalembedwa, "Uthenga sunadze mwa Mawu okha, koma kupyolera mu mphamvu ndi mawonetseredwe a Mzimu Woyera, kukatsimikizira kuti Iye ndi wamoyo."

63 Tsopano, ngati ulipo uthenga wina, monga Paulo anayankhulira kwa limodzi la maguluwo, "Ndine wodabwa kwambiri kuti mwatembenukira ku uthenga wina." Chimene palibenso wina, koma uthenga wodzipangitsa kukhulupirira, ku nthano zachipembedzo, kutembenuka kuchoka ku nkhani yabwino imeneyo.

64 "Ndipo chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala moyo. Ndipo ine ndikukhala mwa inu, ndipo ntchito zimene Ine ndikuzichita," Yohane 14:12, "ntchito zimene Ine ndikuzichita zidzandizindikiritsa Inemwini mwa inu." Ndi Uthenga wotani! Nzosadabwitsa, ife takhalapo ndi dziko lamdima la zaumulungu, koma mu nthawi ya kumadzulo kudzabweranso Kuwala. Padzakhala chiwukitsiro mu nthawi yakumadzulo. Kudzakhala Kuwala pa nthawi ya kumadzulo.

65 Tsopano, chenicheni chomwe cha Uthenga umene unatumizidwa, kuti, "Iye wauka kwa akufa," ife opindula Ake, ife amene tikugawana chiwukitsiro ndi Iyeyo, timatenga zopindula kuchokera ku ichi, potsimikizira kwa dziko kuti Iye ndi wamoyo. Ife sitingachite izo mwa mawu okha. Ife sitingachite izo mwa mwambo wina wa munthu. Ife timangonyezimiritsa ndendende chimene ife tikulozako.

66 Ndiri ndi mantha lero kuti ambiri a ife sitikutengera anthu kwa Khristu. Ife tikuwatengera iwo ku mpingo, ku lingaliro. Koma tikuyenera tiziwatengera iwo kwa Khristu. Iye ndi Mmodzi yekhayo, ndipo Mmodzi yekhayo amene ali ndi Moyo. "Iye amene ali ndi Mwana ali ndi Moyo."

67 Ndipo ngati moyo wa munthu yemwe anafa uwonetseredwa mwa inu, inu mudzakhala moyo womwewo umene iye ankakhala.

68 Ngati magazi a munthu anali a mtundu winawake, ndipo inu munatenga magazi kuchokera kwa munthu mmodzi ndipo nkusintha magazi a munthu mmodziyo kupita mwa wina, iye angakhale mwamtheradi magazi a mtundu umenewo.

69 Ndipo ngati mzimu wanu umene uli mwa inu ukhala wakufa, ndipo inu mwadzozedwa ndi Moyo umene unali mwa Khristu, uli pa inu! Aroma 8:11 anati, "Ngati Mzimu umene unamuwukitsa Khristu kwa akufa, udzakhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi," Moyo womwewo, mphamvu zomwezo, opindula omwewo, amene Iye anali nawo pano pa dziko lapansi, kuchokera kwa Mulungu. Iye anakuwombolani inu, Mbewu imene inadziwidwiratu ndi Mulungu, amene maina awo anaikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

70 Ndipo Kuwala kwa Uthenga kuja kwa chiwukitsiro, chitsimikiziro cha Mawu! Kodi ife tinadziwa bwanji kuti Iye anali Khristu? Chifukwa Iye anatsimikizira zimene Iye anazikamba. Ine ndidzawudziwa bwanji Uthenga wa orali? Mulungu amatsimikizira zomwe Iye analonjeza, ndipo Iye amayankhula za izo. Chimenecho ndi chizindikiritso, kuti ndife opindula limodzi ndi Iye mu chiwukitsiro. Iye amatsimikizira zimene Iye wazikamba.

71 Zimene Iye analonjeza kuti adzazichita mwa Khristu, Iye anazitsimikizira pa chiwukitsiro. Zimene Iye analonjeza kuti

adzachita mmasiku a Mose, Iye anatsimikizira izo. Zimene Iye analonjeza mmasiku a Enoki, Iye anazitsimikizira izo. Mmasiku onse a atumwi, Iye anatsimikizira izo.

72 Tsopano mu tsiku lino, Iye akutsimikizira zomwe Iye ananena, chifukwa izo ziri gawo la Mbewu imeneyo imene inayimiridwa pa Bukhu la Moyo kuti Iye anabwera kuti adzawombole kubwerera kwa Mulungu kachiwiri. Oh, ndi Uthenga bwanji!

73 Mmawa wa Isitala, osati kokha kuti Iye anawuka, koma opindula Ake anawuka naye Iye. Iye. . .Iwo anali mwa Khristu pa kupachikidwa Kwake. Iwo anali mwa Iye pa chiwukitsiro Chake. Ndife opindula Ake, ofulumizitsidwa titatha kufa mu mdima.

74 Dziko lamdima la kusakhulupirira, kumene mipingo ndi zipembedzo, ndi zina zotero, zinali zitatikokera ife kunja. Ndipo munali chinachake mwa ife chikuitanira, "Oh, ife tikufuna Mulungu! Tiri ndi njala ndi ludzu la Mulungu." Ife tinajowina Amethodisti, Abaptisti, Achipentekosite, Apresbateria, ndi zina zotero, ndipo komabe panali chinachake cholakwika, ife timalephera basi kuchipeza Icho. Ndipo zonse mwadzidzidzi, pamene tinali tikupapasa mu mdima, chiwukitsiro chachikulu chinabwera kwa ife mu kuwonetseredwa kwa Mawu olonjezedwa a Mulungu.

75 Monga, Iye anali kuwonetseredwa kwa Mawu olonjezedwa a Mulungu. "Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena, ngakhalenso Ine sindidzalola woyera Wanga Mmodziyo kuti awone chivundi." Iye anawonetsera Iwo, Mawu aliwonse a Mulungu amene analonjezedwa kwa Iye. Iye anatsimikizira izo pamene Iye anawuka mmawa wa Isitala.

76 Tsopano, iwo amene nthawi ina anali kupapasa mu mdima ndi kumangoyendayenda, ngati ndi akuti azitsukana mapazi tsiku *ili*, kapena ngati iwo ndi akuti azisunga tsiku lina, kapena azichita dongosolo linalake la malamulo, zinthu zonsezo zinapita. Pakuti, panali chiwukitsiro chaulemelero chimene chinanyoza chinthu chirichonse chopangidwa ndi munthu chimene munthu anayamba wachitapo, chifukwa chirichonse chopangidwa ndi munthu.

77 Panali pasanakhalepo, mpaka nthawi imeneyo, munthu yemwe akanakhoza kuwuyika pansi moyo wake ndi kudzawutenganso iwo kachiwiri. Iye ananyoza umboni wasayansi uja umene iwo anali nawo, powuka kachiwiri.

78 Pamene iwo anena, kuti, "Yesu Khristu sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse," kuti, "Mphamvu Yake siili chimodzimodzi," kuti, "Uthenga wake siuli chimodzimodzi," pamene Baibulo limanena kuti Iwo ndi chimodzimodzi! Mulungu ananyoza chipembedzo chirichonse, kachikhulupiriro kalikonse, ndipo Iye anasunthira patsogolo ndi Mzimu Wake

Woyera, monga Iye analonjezera, ndipo anatsimikizira izo kwa ife, kuti Iye ndi wamoyo.

79 Ife ndi opindula a chiwukitsiro Chake, ofulumizitsidwa titatha kufa mdziko, mu tchimo ndi zolakwa. "Iye watifulumizitsa ife pamodzi ndi Iye, tinawuka ndi Iye, tsopano tikukhala mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu." Kubweretsa kwake. . .

80 Mzimu Wake ukubweretsanso Moyo Wake womwe womwewo pa dziko lapansi. "Ngati Mzimu wa Mulungu, umene unamuwukitsa Khristu," thupilo, thupi lodzozedwa; ngati Mzimu wa Mulungu unadzoza thupi limenelo mwanjira yakuti, pamene Mbewu imeneyo inagwera mu nthaka, Iye basi sakanamulola Iye kuti apume mmenemo. Ayi. Iye anamufulumizitsa Iye ndipo anamuwukitsa Iye. "Mzimu womwewo," ndi ntchito zomwezo, mwa Mphamvu yomweyo, mwa zizindikiro zomwezo, "kukhala mwa inu, Iwo nawonso udzakuwukitsani inu."

81 Ine ndikufuna kuti ndikuwerengereni inu Lemba laling'ono apa. Ine ndikufuna kuti inu mutsegule ku Lemba lina limene ine ndalilemba apa. Ilo likhoza kukuthandizani inu pang'ono. Ilo likupezeka mu Bukhu la Levitiko, mutu wa 23, ndime ya 9 mpaka ya 11. Mvetserani mwatcheru. Mu chilamulo, chilamulo cha Alevi, Mulungu akuyankhula kwa Mose. Mvetserani. Zinthu zonsezi ndi zoyimira tsopano, ndipo ife tiyima apa kwa mphindi zochepa kuti tilowe mu choyimira ichi.

> *Ndipo Ambuye anayankhula kwa Mose, anati,*
>
> *Uyankhule kwa ana a Israeli, ndipo unene kwa iwo, Pamene* inu. . .*mulowa mu dziko limene Ine ndakupatsani inu,* . . .

82 "Kupita kumalo, malo, amene Ine ndakupatsani inu. Tsopano iwe uyankhule ndi ana a Israeli, kuti pamene mudzafika pa malo enaake awa amene Ine ndakulonjezani inu kuti Ine ndidzakutengani inu, pamene inu mudzafika uko mdziko ili." Tsopano akuyankhula zachithupi apa, kuimira zauzimu.

> . . .*ndipo mudzakolola zokolola mmenemo* (mwalandira chimene Ine ndinakuwuzani inu pamenepo), *pamenepo* inu *muzabweretsa mtolo wa zipatso zoyamba za zokolola zanu kwa wansembe:*
>
> *Ndipo adzaweyula mtolowo pamaso pa Ambuye, kuti udzalandiridwe chifukwa cha inu: pa tsiku lotsatira sabata wansembe adzaweyule iwo.*

83 Ngati pangakhale mwambo woyera uliwonse, umayenera kubwera pa tsiku la sabata, limene linali tsiku lachisanu ndi chiwiri la sabata, limene ndi Loweruka. Koma kodi inu munazindikira, mu chikumbutso ichi, kuwuweyula iwo pa tsiku loyamba la sabata?

84 "Mtolo, umene unali woyamba wa mbewu yako imene unabzala, pamene iyo imera ndi kucha, inu mudzadule mtolo uwu ndi kuwutengera iwo kwa wansembe. Ndipo iye adzawutenge iwo ndi kudzawuweyula iwo pamaso pa Ambuye, ku kulandiridwa kwanu, kuti inu mwalandiridwa. Inu mwabwera ndi mtolo wanu, ndipo iye aweyule iwo pamaso pa Ambuye, pa . . ."

85 Osati pa sabata, tsiku lachisanu ndi chiwiri; koma pa tsiku loyamba, limene ife timalitcha Lamlungu, L-a-m-l-u-n-g-u.

86 Ndithudi, ndiro—liwu la Chiroma, limene iwo ankalitcha ilo tsiku la dzuwa la mulungu wa dzuwa. Koma momwe ilo linasinthidwira!

87 Ilo si d-z-u-w-a panonso. Ilo ndi t-s-i-k-u la M-w-a-n-a, tsiku la Mwana, kuti njere ya Tirigu ija (Mmodzi woyamba wa Mulungu kuwuka kwa akufa) ikuyenera kuweyulidwa pa osonkhana, kuti ife ndi Mbewu Yake; ndipo ndiyo yoyamba ya Mbewu ya iwo amene anagona, yoweyulidwa pa tsiku loyamba la sabata. Pa Lamlungu, Iye anawuka. Anatsanzika bayi-bayi, ndipo anakwera Mmwamba, pamaso pa anthu.

88 Zindikirani, Iyo inali njere yoyamba ya Tirigu wa Mulungu imene inali itaukitsidwa kwa akufa, njere yoyamba ya Tirigu ya Mulungu. Ndi Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu, Mulungu anali atafulumizitsa moyo Wake, kumuwukitsa Iye kwa akufa, ndipo Iye anali Zipatso zoyamba za iwo amene anagona, Chipatso choyamba. Iye anali Mtolo umenewo.

89 Icho ndi chifukwa chimene iwo ankayenera kuti aweyule mtolo umenewo, pakuti iwo unali woyamba umene unafika pa kukhwima. Ndipo iwo unkaweyulidwa ngati chikumbutso cha mathokozo kwa Mulungu, kukhulupirira kuti ena onsewo akanadzabwera. Icho chinali chizindikiro.

90 Ndipo, lero, chifukwa Iye anali Mwana woyamba wa Mulungu kufika pa kukhwima kwathunthu, kuti adzakhale mwa Mulungu, Iye anachotsedwa padziko lapansi ndipo akuweyulidwira pamwamba pa anthu. Oh, ndi phunziro laulemelero bwanji! Mwa Mphamvu yofulumizitsa, Imodzi yoyambayo! Ngakhale, Iye anali—Iye anali ataimiririridwa; ndipo nthawi zambiri, monga ife tiwonere mtsogolo, kuti Iye anaimiririridwa. Koma ichi chinalidi Chipatso choyamba cha iwo amene anagona. Iye anaweyulidwa pa Mbewu yolonjezedwa imene inali ndi lonjezo la Moyo.

91 Iye anadzaweyulidwa pa Tsiku la Pentekoste, "pamene panadza phokoso kuchokera Kumwamba ngati mphepo yoweyula, yamkokomo yamphamvu," ndipo anaweyulidwira pa anthu, anthu achipentekoste amene anali pa Pentekoste, akuyembekezera Mdalitso kuti ubwere.

92 Ndipo kuti tiweyulidwenso, ife tikuzindikira, mu tsiku lotsiriza, malingana ndi Luka 17:30, mu tsiku la

Mwana kachiwiri, "mu tsiku limene M-w-a-n-a wa munthu adzaululidwe," kapena kuweyulidwanso pa anthuwo.

93 Tsopano, Mwana wa munthu ndi Ndani? "Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi, ndipo anadzakhala pakati pathu." Ndipo ngati kuphunzitsa konse kumene ife tiri nako, ndi kutsimikizira kwa Mawu a Mulungu; mwa Mawu a Mulungu, mwa zizindikiro, ndi zodabwitsa, ife tikuziwona lero, kuti mu Bukhu la—la Luka apa, kuti monga ife tangobwereza kumene, kapena—Luka mutu wa 17 ndi ndime ya 30; ndi Malaki 4, ndi Malemba osiyanasiyana amene ife tikuwadziwa, kuti Mawu amenewo akuweyulidwanso pa anthu, kuti miyambo yakufa ya anthu yafa, ndipo Mwana wa Mulungu ali moyo kachiwiri ndi ubatizo wa Mzimu Woyera pakati pathu pomwe, ndipo akutipatsa ife Moyo.

94 Monga Khristu anali Mmodzi woyamba kuwuka, kuchokera kwa aneneri onse, ndi ena otero; ngakhale anaimiridwa mmalo ambiri, Iye anali Zipatso zoyamba za iwo amene anagona. Mwa Mkwatibwi, kubwera kwa Khristu, kutuluka kuchokera mu mpingo, payenera kudzakhala Mtolo woweyulidwa kachiwiri mmasiku otsiriza. Oh, mai!

95 Kuweyula kwa mtolo! Kodi mtolo unali chiyani? Woyamba amene anafika pokhwima, woyamba amene anatsimikizira kuti anali tirigu, amene anatsimikizira kuti anali mtolo.

96 Aleluya! Ndikutsimikiza kuti mukuona zimene ndikuzikamba. Iwo unkaweyulidwa pa anthu. Ndipo nthawi yoyamba padzatulukira, kwa m'badwo wa Mkwatibwi, kwa chiwukitsiro kuchokera mu zipembedzo za mdima, udzakhala Uthenga, kuti kukhwima kwathunthu kwa Mawu kwabwereranso mu Mphamvu Yake yonse, ndipo akuweyulidwa pa anthu, ndi zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa zimene Iye anachita kumbuyo uko.

97 "Pakuti Ine ndiri ndi moyo, inunso mudzakhala ndi moyo," akuyankhula kwa Mkazi Wake. "Chifukwa Ine ndiri moyo, inunso mudzakhala ndi moyo." Chinali chiwukitsiro chotani chimenecho! Ndipo ndi chiwukitsiro chotani ichi, kukafulumizitsidwa kuchoka kwa akufa, "kukapangidwa kukhala wamoyo mwa Khristu Yesu," ndi Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu!

98 Iye anaweyulidwira kwa iwo. Mawu, amene Iye anali, anaweyulidwira kwa iwo pa Tsiku la Pentekoste, Mawu anawonetseredwa. Tsopano, ndipo monga ine ndikunenera, Iwo akuyenera kuweyulidwa kachiwiri mu tsiku lotsiriza. Tsopano, mwachitsanzo. . .

99 Inu mukuti, "Chabwino, tsopano, dikirani miniti, M'bale Branham. Ine ndikudziwa mpingo umene. . ." Chabwino, ine ndikutero, nanenso. Mukuona?

100 Koma tsopano, mwachitsanzo, bwanji ngati—ngati tikanati tikubwerera ku Tucson madzulo ano, tsopano, ndipo mmodzi aliyense wa ife anali ndi . . . anali woti alowa mu a—Cadillac yaikulu, yatsopano? Ndipo mipando yonse inapangidwa kuchokera ku—chikopa cha gwape, chikopa chofewa kwambiri, yofewa komanso yophweka kukhalapo; ndipo mabolodi a pansi anali a nsalu; chiwongolerocho chinali chokutidwa ndi siliva ndipo chinali ndi zitsulo za diamondi paliponse; ndipo injiniyo inayesedwa ndi makina kuti inali injini yabwinobwino; ndi magudumu anali . . . onse anali ndi mabering'i ndipo anali opakidwa girizi; ndipo matayala onse anali osabowoka ndipo osaphulika; ndipo onse anayesedwa mwasayansi.

101 Iwo anali atakankhidwira kunja pamene amakonzerapo, awiri onsewo, ndipo awiri onsewo anali atadzaza mafuta. Imeneyo ndi mphamvu yoyendetsera, mafuta, chifukwa mmenemo muli octeni. Koma tsopano pamene muzifuna kuwaliza iwo, ngakhale awiri onsewo akuwoneka ofanana, koma pali imodzi mwa iwo ilibe kuthetheka kulikonse, mphamvu yoyatsira.

102 "Chabwino," inu mukuti, "mphamvu imakhala mmafutawo, M'bale Branham." Koma ine sindikusamala kuchuluka kwa mphamvu imene ili mmafuta; pokhapokha ngati patakhala kuthetheka pamenepo kuwonetsera mphamvu imeneyo, pokhapokha patakhala mphamvu pamenepo yoti itsimikizire kuti amenewo ndi mafuta, akhoza basi kungokhalanso madzi. Mpaka . . .

103 Ziribe kanthu ndi mochuluka bwanji momwe azaumulungu amadzinenera, momwe inu mwakhazikitsira bwino mpingo wanu, ndi maphunziro ochuluka bwanji amene inu muli nawo, ndi mochuluka bwanji monga Baibulo; mpaka Mtolo woweyulidwawo, mpaka Mzimu Woyera utabwera pa munthu ameneyo kuti udzawafulumizitse Mawu amenewo! Mafuta amaimira Mawu. Iwo ndi Choonadi; koma, popanda Mzimu, Iwo sangasunthe.

104 Ife tatsindika kwambiri pa Zimango ndipo wopanda kalikonse pa Mphamvu. Iwo amasowa Mphamvu yoyendetsera ya Mulungu, Mphamvu ya chiwukitsiro ya Yesu Khristu pa Mpingo, kuti ikawonetsere ndi kukwaniritsa kuti *Awa* ndi mafuta. Iwo akhoza kukhala mu chigubu cha mafuta; iwo akhozabe kukhala ali madzi, mwaona. Koma chitsimikiziro chokhacho cha izo, ndi, kuyika Moyo uwu pa izo, ndipo Iwo adzatsimikizira ngati ali mafuta kapena ayi.

105 Ndipo pamene muyesera kuti muyike Mzimu Woyera mu chipembedzo, mumakhala ngati mukuyesetsa . . . Inu mukhoza kukhala ndi kuphulika; mungawononge injini yanuyo, poyidzazitsa iyo ndi utsi.

106 Koma, oh, ndine wokondwa kuti kuli Mphamvu za octeni teni sawuzande, Mawu a Mulungu ndi Mzimu Woyera zoti ziyatse Iwo, ndi kuwukitsa Mphamvu ya Mulungu mmoyo wa mwamuna, kapena moyo wa mkazi, kapena mu mpingo. Iyo inakankhira Cadillac iyo kupita kumusi pa msewu kutali, pansi pa Mphamvu yoyendetsera ya Mzimu Woyera imene inabwerera ndipo inaweyulidwa pa anthu pa Tsiku la Pentekoste, kumupanga Iye yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

107 Apo panali Mtolo woyamba umene unabwera kuchokera kwa aneneri onse, yemwe anali Mwana wa Mulungu, Mfumu ya aneneri onse.

108 Pakhala pali mipingo, mipingo, akwatibwi, akwatibwi, mipingo, akwatibwi, akwatibwi.

109 Koma pakuyenera kudzabwera Mmodzi! Aleluya! Pakuyenera kudzabwera Mkwatibwi weniweni! Pakuyenera kudzabwera Mmodzi amene alibe Zimango zokha, koma Zimphamvu za Izo, zimapangitsa Mpingo umenewo kukhala wamoyo, kumasunthira mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Mpaka titadzafika pa malo amenewo, mpaka titadzawapeza malo amenewo, nchaubwino wanji kupukuta mahabu? Nchaubwino wanji kuyipatsa iyo ntchito yosintha kawonekedwe kapena ntchito yoipolisha, pamene mulibe Zimphamvu mmenemo? Ziribe kanthu ndi Zimango zingati zikutsimikizira kukhala zolondola, payenera kuti pakhale Mphamvu yoti ipangitse Izo kugwira ntchito.

110 Icho ndi chimene Iye anatsimikizira! Aleluya! Icho ndi chimene Isitala inatsimikizira. Iye sanali kokha Mawu, koma Iye anali Mulungu Iyemwini, Mphamvu, mu Mawu. Izo zinapanga thupi la Yesu Khristu (lozizira, lowuma, ndi lakufa, mmanda) kugwedezekera mu Moyo ndi kuwuka kachiwiri, ndi kugudubuza mwalawo. "Ine ndi Iye amene ndinali wakufa," wakufa kwambiri mpaka dzuwa linati Iye wafa, mwezi unati Iye wafa, nyenyezi zinati Iye wafa. Chirengedwe chonse chinati Iye wafa. Ndipo tsopano dziko lonse liyenera kuti lizindikire kuti Iye ndi wamoyo kachiwiri. Iye sanali kokha Zimango, Mawu a Mulungu, Iye anali Zimphamvu zotsimikizira Izo.

111 Ndipo monga Iye, pokhala Mkwati, Mkwatibwi ayenera kutulukira, chifukwa Iye ndi gawo la Iye. Ndipo Izo zikhoza kungokhala kuwonetseredwa kwa kukwaniritsidwa kwa mavumbulutso onse amene aliyense anayankhulapo za Mkwatibwi; Izo zikhoza kungowonetsera. Ngati izo zichita chinachake chosiyana ndi Mkwati, izo si Mkwatibwi. Chifukwa, Iye ali mnofu wa mnofu Wake, fupa la fupa Lake; Moyo wa Moyo Wake, Mphamvu ya Mphamvu Yake! Mkaziyo ndi Iye! Monga mwamuna ndi mkazi ali mmodzi, ndipo mkazi kutengedwa kuchokera ku mbali yake, Iye anatenga Mzimu, Mzimu

wachikazi, kuchokera kwa Iye. Mnofu kuchokera kumbali Yake, zinapanga ziwiri zonse Zimango ndi Zimphamvu, Mkazi. Mzimu wa Iye ndi mnofu wa Iye, ndi kuziyika izo pamodzi, ndipo anapanga Zimango ndi Zimphamvu. Mpaka mpingo kapena anthu. . .

112 Akalulu onse a Isitala awa, ndi miyambo, ndi mipingo yayikulu, ndi zokongola, zidzalephera ndi kutha.

113 Mpaka Mpingo umenewo utadzakhala ziwiri zonse Zimphamvu ndi Zimango; ndipo Mzimu wa Mulungu, umene unamusuntha Iye, kuti azichita zinthu zimene Iye ankachita! Ngati Iye anagunda pa masilinda sikisitini, Mkwatibwinso adzatero. Ameni! Pakuti Iye anati, mu Yohane 14:12, "Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita. Ine ndidzampatsa iye ulamuliro wa Zimphamvu Zanga, mu Zimango zake, kuti dziko silidzatha kupirira nazo izo; ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye kachiwiri pa tsiku lomaliza." Umenewo ndi Uthenga wa Isitala, Zimphamvu ndi Zimango, pamodzi! Zimango zopanda Zimphamvu, sizimakhala zabwino; ngakhalenso Zimphamvu, zopanda Zimango.

114 Inu mukhoza kukuwa ndi kufuula, ndi kulumpha mmwamba-ndi-pansi, zonse zimene inu mukufuna kutero, ndi kukana Mawu awa, izo sizingachite ubwino uliwonse. Inu muzingoliza pamenepo—mapistoni a. . .Kuthetheka kulipo pamenepo kuti kuyatse, koma mulibe mafuta oti muyatsire iyo.

115 Izo zimangogwira ntchito pamene izo zibwera pamodzi. Ameni! Chotero, chimodzi chimatsalira, ndipo Chinacho chimapita mmwamba. Ndicho chinthu chokhacho chimene chiripo kwa izo. Komabe, ziwiri zonsezo zikhoza kumawoneka zofanana, ziwiri zonsezo kumadzinenera kuti ndi mipingo, ziwiri zonsezo kumadzinenera kuti ndi Mkwatibwi. Koma Wina ali ndi Zimango *ndi* Zimphamvu, Izo zimapangitsa izo kuchitika, za zomwe Iye ananena kuti ndi Choonadi.

116 Izo sizingasunthe basi, ziribe kanthu momwe Zimango ziriri zabwino, mpaka Zimphamvu zitabwera. Pamene Zimphamvu zibwera, Moto umenewo umapangidwa kuti ulumikizike ndi octeni mu mafutawo. Ndipo pamene Izo ziphulika, izo zimayambitsa kuyaka, ndipo kuyaka kumeneko kumasuntha kuyenda kulikonse, kusuntha kulikonse, pakuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndicho chiwukitsiro. Imeneyo ndiyo Mphamvu yeniyeni ya Mulungu, Zimango ndi Zimphamvu. Zindikirani, "Ndi Mzimu umene umafulumizitsa." Ndi—ndi Kuthethekako kumene kumayatsa. Si mafuta amene amayatsa; ndi Kuthethekako kumene kumayatsa mafutawo. Mukuona?

117 "Inu simungathe kuchita kanthu popanda Ine; koma ndi Ine mukhoza kuchita zinthu zonse." Monga Iye ali Mawu, Iwo ndi Atate akukhala moyo. "Atate ananditumа Ine, chotero

Ine ndikukutumani inu. Monga Atate andiyatsa Ine ndi kundikankhira Ine mu chirichonse, Ine ndimachita chokhacho chimene chiri chokondweretsa kwa Mulungu. Tsopano, monga Iye ananditumа Ine, chomwechonso Ine ndikutumani inu ndi Zimango zomwezo, ndipo zimatengera Zimphamvu zomwezo kuti zizichita Izo. Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene amadzinenera kuti ali ndi Zimango. Zimphamvu zidzatenga malo Ake."

118 Paulo anati, "Uthenga unadza kwa ife osati mwa Mawu okha," kudzera mmafuta okha, "koma kudzeranso mu Kuthetheka," kuwupangitsa Iwo kusuntha. Ndi zimenezotu. Iwo unabwera kwa ife mwanjira imeneyo.

119 Ndi Mzimu womwewo, umene unamuwukitsa Iye, umene unafulumizitsa wokhulupirira woona ku Moyo Wamuyaya. Tsopano kumbukirani, mwakuyankhula kwina. . . Tsopano penyani, pamene ife tikuchoka mu nthawi yathu. Zindikirani, "Mzimu womwewo," tsopano, Aroma 8:1. Tsopano tiyeni tingowerenga izo kachiwiri, mu Aroma 8:1, ndipo ife tiwona chimene iyo ikunena. Chabwino. Ndipo osati Aroma. . . Ine ndimatanthauza, 8:11, pepani.

120 Mu Aroma 8:11, "Koma *ngati*. . . " Ndi pamene pali vutopo. Apo ndi pamene akugwira Iye.

> *Koma ngati Mzimu wa iye* (Mulungu, Mzimu Woyera) *amene anamuwukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu*, . . .

121 Tsopano, ndi zimenezotu, "Ngati Mzimu wa Mkwati ukhala mwa Mkwatibwi!"

122 Pamene Mulungu anampanga mkwati Wake woyamba, Iye anampanga mkwati poyamba, ndipo iye anali ziwiri zonse mwamuna ndi mkazi, mu mzimu; anamuwumba iye mu fumbi la dziko lapansi, kuti amupange iye kukhala chogwirika. Ndipo zindikirani pamene Iye anamupanga Eva, kuchokera kwa Adamu, Iye sanatenge chidutswa china cha dongo, Iye anatenga kuchokera ku chidutswa chomwecho cha dongo; Mawu omwewo, pakuti Adamu anali Mawu olankhulidwa. Mukuona? Iye anatenga kuchokera kwa iye, ndipo kenako anatenga. . . Iye anali ndi mzimu wachimuna ndi wachikazi. Ndipo Iye anachotsa mzimu wachikazi kuwuchotsa kwa Adamu, ndipo anadzawuyika iwo mwa Eva; chotero ilo likadali gawo la mzimu wa Adamu, ndi thupi la Adamu. Kenako, unali mzimu wa Adamu, mphamvu, imene inafulumizitsa zimango za thupi lake.

123 Chotero Mkwatibwi akuyenera nayenso kukhala mnofu wa mnofu Wake, ndi fupa la fupa Lake. Ndiye mnofu wachivundi uwu udzakhala bwanji thupi Lake? Ife tifika kwa izo mu miniti, mwaona. Kodi izo zimachitika chotani? Chotani? Kodi kusandulika kwakukulu kumeneku ndi chiyani? Zindikirani.

> Tsopano *ngati Mzimu wa iye* (Mulungu) *amene anamuwukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu, iye amene anamuwukitsa Khristu kwa akufa adzafulumizitsanso matupi anu achivundi ndi Mzimu Wake umene ukukhala mwa inu.*

124 Oh, mai! Mmodzi wokonzedweratuyo, ndithudi, monga Mbewu inasiyidwa pa dziko lapansi, Mmodzi amene anali ndi Moyo mwa iwo. Ambiri a iwo anali atafa; iwo anali mbewu yovunda chabe; madzi ndi zinthu zinawotcha iwo. Koma, inu mukudziwa, apo panali Mbewu itagona pamenepo yokonzekera Moyo. Mulungu ankadziwa kuti Iyo inali pamenepo.

125 Tsopano, okonzedweratu Awo ndi amene adzakhale oyambirira kudzafulumizitsidwa ndi Mzimu Woyera, pakuti Mzimu Woyera umabwera kudzatenga Ake Omwe. Tsopano, izi ndi zakuya tsopano, ndipo muwonetsetse kuti mwazimvetsa izi bwino bwino.

126 Tsopano, monga dzuwa linatumizidwa kudutsa pa dziko lapansi, osati kuti lidzabweretse miyala, imene inali dothi nayonso, ku moyo, ilo silinali kuti lidzabweretse dothi lonse kukhala lamoyo, koma kunali kuti lidzabweretse gawo la dothi limene linali mozungulira moyo.

127 Si anthu onse amene adzamulandire Khristu. Oh, ayi. Koma iwo amene Mulungu anawadzozeratu Moyo, akusungidwa mozungulira lina la dothi la m'nthaka, amenewo ndi Amene Iye akubwera kudzawafulumizitsa. Iwo ndi Amenewo.

128 Kuti, tsopano, dothi limenelo likanadzakhala pamenepo padzuwa, ndi kuti, "Oh, dzuwa lakale ili likutentha kwambiri!" Mwala umenewo, nkuti, "Dzuwa lakale limeneli likutentha kwambiri!" Koma mbewu yaying'onoyo, inati, "Ichi ndi chimene ine ndikufuna," ndipo inayamba kuphukira kumoyo. Iyo inafulumizitsa gawo ilo la dothi. Chifukwa, dzuwa linatumizidwa osati kuti lidzafulumizitse thanthwe, osati kuti lidzafulumizitse dothi, koma kuti lidzafulumizitse moyo wa mbewu.

129 Tsopano, Mzimu Woyera ukubwera tsopano. Ndithudi, Iwo sunatumizidwe. . . Chifukwa chiyani anthu onse sadzawulandira Iwo? Iwo sunatumizidwe kwa iwo.

130 Munthu wina anandiuza ine, "Ine sindimakhulupirira. Sindikusamala chimene inu munganene. Ngati inu mungadzutse akufa, kapena chirichonse, ndi kuchiritsa odwala, ndi kutsimikizira Iwo mwanjira iliyonse, ine sindingakhulupiririrebe Iwo."

131 Ine ndinati, "Ayi ndithudi. Ndinu wosakhulupirira. Iwo sutanthawuza kanthu kwa inu. Iwo sunatumizidwe nkomwe kwa inu. Iwo unatumizidwa kwa iwo amene adzakhulupirire."

132 Uthenga ndi wa kwa wokhulupirira. Kwa iwo owonongeka, Iwo ndi zopusa; koma kwa iwo amene ali mwa Khristu, ndi gawo la Mbewu imeneyo, Iwo ndi Moyo.

133 Nkhani yanga yaying'ono ya mlimi akuyika dzira pansi, kapena dzira la mphungu pansi pa nkhuku. Mukuona? Mphungu yaing'ono ija inali, mwamtheradi, iyo inali—iyo inali yowoneka-mosamvetseka, cholengedwa chaching'ono. Pamene mlimi uyu anachita chinthu chimenecho chimene iye anachita, kuyika dzira la mphungu ili pansi pa nkhuku yakale iyi. Ndipo iyo inaswa nkhuku yowoneka-modabwitsa, ndipo iyo inali—inali yosamvetseka, yaying'ono. Iyo sinkawoneka ngati iwo. Nthenga zake sizinali ngati zina zonsezo, ndipo iyo—iyo basi . . . Iyo inali yosamvetseka, yaying'ono. Ndipo nkhuku zina zonsezo zinaizindikira iyo ngati yosamvetseka. Ndipo nkhuku inazungulira . . .

134 Iyo sinkakonda zakudya zimene iyo inkayidyetsa. Iyo basi sinkakonda kupalasa kumeneko mu kholamo. Iyo, iyo inalibe kanthu koti ichite ndi izo. Chotero iyo inkadabwa chifukwa chimene iyo inkayenera kukhala yokhayo yosamvetseka kumeneko, mulimonse. Mukuona? Ndipo iyo sinalawe chirichonse chimene . . . Iyo inkangodya zokwanira kuti ziyisunge iyo kukhala yamoyo, chifukwa iyo sinkakonda kukoma kwake, mwaona. Chifukwa, iyo siinali nkhuku, kuyamba ndi kuyamba. Mukuona?

135 Ndipo a—nkhuku imalira, ndipo, inu mukudziwa, "Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu choterocho. Kujowina mpingo." Izo basi sizinkamveka bwino, ndi kanthu kakang'onoko. Chotero iye amazitsatira nkhukuzo pamenepo mpaka tsiku lina amayi ake . . .

136 Mphungu yakaleyo inadziwa kuti iyo inali itayikira mazira ochuluka kwambiri, ndipo panali limodzi limene limasowa. Iyo inkadziwa kuti mphungu imeneyo inali kwinakwake, chotero iyo inayamba kusakasaka iyo. Ndipo iyo inazungulira pamwamba pa phiri, ndi kumusi mu zigwa, ndi kulikonse kumene iyo ingakhaleko. Pofika nthawi iyi, iyo, ndi nthawi yoti iyo ibadwe. Ndi nthawi yoti igogomoledwe. Inati, "Mwinamwake khwangwala anabwera ndipo anadzanyamula dzira langa; mwinamwake khungubwe. Ine sindikudziwa. Chinachake chinadzatenga dzira langa. Koma ine ndikudziwa . . . Dzira limenelo liri mmalingaliro anga. Ine ndiri ndi mwana wamwamuna kwinakwake. Ine ndikuyenera kuti ndimusake iye."

137 Mulungu amachitanso chomwecho. Iye ndi Mphungu Yaikulu imeneyo. Mmaganizo Ake Iye ankadziwa kuti Iye adzakhala ndi Mpingo. Iye ankadziwa kuti Iye adzakhala ndi anthu. Ziribe kanthu chimene chawakumbatira iwo,

ziribe kanthu kuti iwo anawutamiridwa pansi pa chiyani, Iye akusakasaka. Iye akusakasaka Ake Omwe.

138 Ndipo tsiku lina, nkhani ikuti, mphungu yakale iyi inawulukira pamwamba pa khola. Iyo inkayang'ana paliponse, ndipo iyo inamupeza iye. Oh, chifukwa cha chiwukitsiro chimenecho, kuti izindikire kuti iyo sinali nkhuku, pambuyo pa zonsezo. Iyo inali mphungu! Ndipo iyo nthawizonse inkaphunzitsidwa kuti iziyang'ana pansi, kuyang'ana tizirombo kapena chinachake mu kholamo. Koma iyo inamva kukuwa, kumene kunati, "Tayang'ana mmwamba mbali *iyi*!" Ndipo iyo inayang'ana pamwamba pake, ndipo apo panali cholengedwa chokhala ndi mapiko mapazi fortini, champhamvu-ko kuposa nkhuku zonse zimene zinali mu kholamo, ndipo chinadzinenera kuti iye ndi mwana wake.

Iyo inati, "Amayi, ndingafike bwanji kwa inu?"

139 Anati, "Ungolumpha, yamba kukupiza mapiko akowo, pakuti ndiwe mphungu."

140 Mwaona, iyo inkadziwa kuti iye anali ndi mwana kwinakwake. Ziribe kanthu kuti iye analeredwa ndi chiyani, iye ali ndi mwana wamwamuna kwinakwake.

141 Ndipo Mulungu amadziwa! Aleluya! Iye ali ndi wokonzedweratu, Mpingo wodzozedweratu! Iye ankadziwa kuti Iye ali ndi ana aamuna ndi ana aakazi, ndi Mkwatibwi, akudikirira penapake; pamene Mzimu Woyera uyamba kuwulukira pa iwo, Mtolo woweyula umenewo. Oh, mai! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Osati nkhani yopeka, koma chenicheni!

142 Ziribe kanthu ndi angati anayesetsa kumuwuza iye, "mphungu," iyo sinkadziwa chimene mphungu inali. Komabe, iyo inali mphungu. Iyo sikanamvetsa izo mpaka iyo itawona chinachake chimene chinanyezimiritsa iyo, chimene iyo inanyezimiritsa, kani.

143 Ndipo pamene ife tiwona, osati chipembedzo, osati Ph.D., osati LL.D., osati mnansi wabwino; koma mwana wa Mulungu wowumbidwa mu chifanizo cha Mulungu, ndi Mphamvu yoyendetsa ya Mulungu kuti ayankhe pempho la tsiku lino, kuti Iye ndi yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, palibe nkhuku imene ingakugwire iwe. Iyo imasaka Amayi ake. Iyo ndi mphungu, kuyamba ndi kuyamba. Iyo imazindikira. Mphungu yeniyeni iyi imazindikira kuyitana kwa Mawu a Mulungu. Chifukwa chiyani? Iye ndi mphungu. Mphungu kwa mphungu! Mawu maziko asanakhazikitsidwe, Mawu ku Mawu! Mawu, okonzedweratu, ku Mawu olembedwa a ora. Iwe umazindikira malo ako. Iye amawasaka Iwo.

144 Ichi ndiye, thupi lapadziko ili, limafulumizitsidwa ndi kubweretsedwa ndi Mzimu wofulumizitsa wa Mulungu ku kumvera ku Mawu a Mulungu.

145 Mwamsanga. Pamene iyo inkafuna kuti idziwe momwe iyo ingafikire kumeneko ndi iyo, iyo inali itaphunzitsidwa kuti iyo sikanakhoza kuchita zimenezo. "Iwe sungathe kupita mmwamba kuposa momwe ungalumphire." Iyo ndi nkhuku. Mukuona?

Koma mphungu iyi inati, "Izo siziri chomwecho."

"Chabwino, taziwonani nkhukuzo!"

146 "Ziribe kanthu chimene nkhuku ziri, ndiwe mphungu. Ungoyamba kutambasula mapiko amenewo, ndi kuchita masewera olimbitsa thupi pang'ono. Yamba kusunthira mmwamba!"

147 Mawu ku Mawu! "Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita." Mukuona? "Chifukwa ine ndiri moyo, iyenso adzakhala moyo." "Ndipo ngati Mzimu umene unamuwukitsa Iye kwa akufa ukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsa thupi lanu lachivundi." Mukuona?

148 Kodi Iwo umachita chiyani? Tsopano tamverani, kuti inu mudziwe. Ndipo Isitala iyi, ine ndikufuna kuti iyo itanthauze mochuluka kwa inu kuposa momwe Isitala iliyonse inayamba yachitirapo. Mukuwona? Ine ndikufuna inu muwone zimenezo. Ife tikudziwa chimene Iwo unamuchitira Iye; koma ine ndikufuna kuti inu muwone zimenezo, osati udzachita, Iwo wakuchitirani inu chomwechonso. Mukuona? Kodi Iwo umachita chiyani? Iwo umafulumizitsa thupi lachivundi. Thupi lachivundi ili limene ife tikukhalamo, Iwo umafulumizitsa ilo, mwa kuyankhula kwina, kulibweretsa ilo ku Moyo.

149 Tsopano, inu amene nthawi ina munayendapo ndi ndudu yayikulu kwambiri ili pakamwa panu, ndi chirichonse, kapena mpukutu wa ndudu; ndi akazi inu amene nthawi ina munali ndi tsitsi lalifupi, kuzipenta, ndi kumapitirira, ndi kumavala zazifupi, ndi zinthu monga zimenezo; zonse pakamodzi, Chinachake chinafuula, ndipo inu munayang'ana pansi apa ndipo Iwo anali Mawu. Mwaona, Iwo anafulumizitsa anu... Inu munati, "Palibenso akabudula kwa ine, palibenso mowa kwa ine, palibenso kunama, palibenso kuba, palibenso *izi, izo*." Mukuona? Mzimu umene unamuwukitsa Iye kwa akufa, ukukhala mwa inu, udzabweretsanso matupi anu achivundi, fumbi la dziko lapansi, kubwera mukumvera. Inu mukuona? Ndi chiyani chimenecho? Kumvera chiyani? Khristu. Khristu ndi ndani? Mawu. Osati fioloje, koma Mawu!

150 Ndiye inu mukunena, kuti, "Zinthu izi, oh, ine ndikuganiza izo ziri bwino kuti akazi azivala mathalauza."

151 Pamene, Mawu anati, "Ayi." Mwaona, Iwo amakufulumizitsirani inu kwa Iwo. Mukuona? Inu mumakokeredwa kwa Iwo. Mwaona, ndi inuyo, ndiye. Iwo

amadzakhala. . .Inu mumadzakhala gawo la Mawu. Iwo amabweretsa thupi lanu, osati. . .

152 Chabwino, inu mukuti, "Chabwino, tsopano, ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chinachake. Abusa anga. . ." Ine sindikusamala chimene abusa anu ananena; ndi chimene Mawu akunena! Ngati inu mukufuna kuti mukhale nkhuku, pitirirani ndi iwo. Koma ngati abusa akuyankhula zosiyana ndi Mawu awa, ndiye iwo si wodyetsa mphungu; uh-huh, iwo ndi wodyetsa nkhuku, mwaona, osati a mphungu. Mukuona? Mphungu imadya pa Chakudya cha mphungu. Mukuona? Icho chimafulumizitsa!

153 Baibulo linati ndi zolakwika kuchita zimenezo, ndipo mwamuna ndi ena otero ndi zonse zimene inu mumachita, ndi zolakwika. Kumati, "Masiku a zozizwitsa anapita." Baibulo ili linati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ngati iwo anena kuti, "Kumeneko ndi kuwerenga maganizo. Ndipo ndi mtundu wina wa kuwerenga malingaliro, kuzindikira za mumtima uku. Ndi masomphenya onse awa ndi zinthu, ndi zamkutu," mwaona, iwo ndi nkhuku. Iwo sakudziwa chimene Chakudya cha mphungu chiri.

154 Koma, m'bale, pamene inu mumva kufuula kuja, pamakhala Chinachake mwa inu! Ndinu mphungu, kuyamba ndi kuyamba. Chifukwa chiyani? Inu ndinu Mbewu imeneyo, imene chiwukitsiro cha M-w-a-n-a chatulukira, ndipo Mtolo woweyula uli pa dziko lapansi, kudzakupangitsani inu kuzindikira kuti ndinu mphungu ndipo osati nkhuku yachipembedzo. Inu mukuona zimenezo? Hah!

155 "Ngati Mzimu umene unamuwukitsa Iye kwa akufa," Mawu, Mphamvu ya Mawu, "ukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi." Tsopano ife tikhala bwanji mnofu wa mnofu Wake ndi fupa la fupa Lake? Chifukwa, mwamsanga, pamene ife tikadali ochimwa achivundi, achivundi, okonzeka kuti tife, matupi awa, Iwo unadzafulumizitsa thupi limenelo. *Kufulumizitsa* ndi chiyani? "Kubweretsa ku Moyo." Mzimu umene nthawi yina unkakonda kumwa, kuthamanga uku ndi uku, kuchita chigololo, ndi zonse izi, iwo wafulumizitsidwa; bwanji, chinthucho chinafa, ndipo inu mwaukitsidwa. Iwo umafulumizitsa thupi lanu lachivundi.

156 Chotero, matupi anu ndi kachisi wa Zimphamvu, chifukwa (bwanji?) kuyambira pachiyambi inu ndi gawo la Zimango. Oh! Ndi chimenecho chiwukitsiro chanu. Ndi umenewo Mpingo mu chiwukitsiro, limodzi ndi Iye. Matupi awa pakali pano afulumizitsidwa. Mwaona, inu mwamva; inu mukukhulupirira. Izo zinakusinthani inu kuchoka ku chipembedzo kupita ku Mawu. Mukuona?

157 Zimphamvu, ngati Izo zibwera pa madzi, iwo amangokhavuka, "Masiku a zozizwitsa anapita." Pompu-

pompu-pompu, "Oh, ndimakhulupirira Baibulo," pompu-pompu-pompu, "koma apo—apo palibe ayi . . . " Pompu-pompu-pompu! Mukuona?

158 Koma pamene Iye anadzagunda octeni wani sauzande, "Whrruuu," kutali iye anapita, mwaona. Momwe, mai, Zimphamvu zikakantha Iwo! Koma Iyo ikakantha nkhuku, izo sizingachite ubwino uliwonse. Koma pamene Iyo ikantha mphungu, iyo imanyamukapo. Ameni! Zimphamvu ndi Zimango! Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndiko kuti, ngati iye ali mphungu yowona tsopano, iye "adzamvetsa."

159 Ndiloleni ine ndikuwongolereni Lemba laling'ono apa. Ine ndikuganiza kuti tachoka pa foni, koma ife tikadali pano. Yohane Woyera 5:24, Yesu anati, "Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo wosatha." Tsopano taonani, ine ndimapita uko mu msewu ndi kukangotenga izo momwe ziliri, chimene Iwo ali, popanda kumvetsa kwauzimu . . . Osawapangitsa Iwo kunena china chirichonse, koma kungonena chimene Iwo akunena, mwaona, mawu olondola pamenepo, mu Chigriki, mu chapachiyambi, iwo amati, "Iye amene amvetsa Mawu Anga."

160 Tsopano, kuti titsimikizire kuti izo nzoona. Ine ndimapita kumusi kuno, ndipo apa pali woledzera akubwera mu msewu, ndipo ali ndi mkazi wa mwamuna wina mmikono mwake, ndipo akutukwana, ndi kutchula Dzina la Mulungu pachabe, ndi china chirichonse monga choncho. "Ndikuti, kodi inu munamva chimene mlaliki uja ananena? Kodi munatero?" "Eya, ine ndinamva Izo!" Izo sizikutanthauza kuti iye ali nawo Moyo Wamuyaya. Mukuona? Mukuona?

"Iye amene amvetsa Mawu Anga," iye amene ali mphungu!

161 "Tsopano, M'bale Branham, ine ndikufuna Malemba ochuluka kuposa amenewo."

162 Chabwino, "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa. Mlendo sizingamutsatire."

163 Monga mu nkhani ya *Chikwati Ndi Chilekano*, tsiku lina. Pamene Mzimu Woyera unandiuza ine zimenezo, ine ndinabwera kudzanena izo basi momwe Iye anandiwuzira ine.

164 Mtumiki wina wamkazi anandipatsa ine chidzudzulo chakuthwa, pang'ono. Iye anati, "Ine ndikuganiza inu mwatenga malo a Mulungu?"

Ine ndinati, "Ayi, mayi."

165 Anati, "Chabwino, inu munawauza iwo kuti tchimo lawo lakhululukidwa." Ndinati, "Kuti?" Ndinati, "Mulungu yekha ndi amene ali ndi mphamvu." Mwaona, Mfarisi wina. Mukuona? . . ? . . .

166 Ine ndinati, “Inu mwaona, kuti inu mudziwe, kuti, Yesu anamuwuza Petro ndi atumwi, iye atatha kukhala ndi vumbulutso la Yemwe Iye anali.”

Iye anamuwuza Iye, “Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu.”

167 Iye anati, “Ndiwe wodala,” mwaona, “mwana wa Yonasi; thupi ndi mwazi sizinawululire Izi kwa iwe, koma Atate Anga amene ali Kumwamba awululira Izi. Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga; zipata za gehena sizingawugonjetse Iwo. Ndipo Ine ndikukupatsa iwe mafungulo; chimene uchimanga pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga Kumwamba; chimene uchimasula padziko lapansi . . . ”

168 Ndiro vumbulutso Lauzimu lija la Mawu osandulika thupi. Ngati Iwo anali thupi mu tsiku limenelo mwa Mwana, Mkwati, Iwo ndi thupi lero mwa Mkwatibwi. Mukuona? “Machimo a aliyense amene muwakhululukira, kwa iwo akhululukidwa; machimo a aliyense amene inu muwasunga, kwa iwo asungidwa.”

169 Tsopano, mpingo wa Katolika unazitenga zimenezo ndi kuzitengera izo kwa ansembe awo, koma izo ndi zachithupithupi.

170 Penyani, anali auzimu, Mawu owululidwa amene anachita izo!

171 Ndi chifukwa chake Iye anawauza iwo kuti apite kukabatiza mu “Dzina” la Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Iye ankadziwa kuti iwo ankadziwa Yemwe Iye anali.

172 Ndikuyankhula ndi mlaliki wamng’ono tsiku lina, iye anati kwa ine, iye anati, “Tsopano, M’bale Branham, ine ndinatuluka ndi kudzajowina, ndinapita ku mpingo *wakuti-wakuti*, mpingo wa Chipentekoste.”

173 Kumene, Achipentekoste tsopano ayamba kudya mkate wozungulira, inu mukudziwa. Inu munamva za zimenezo, ine ndikuganiza; mkate wopanda chotupitsa, mulungu wa mwezi, inu mukudziwa. Ndipo onsewo anavomereza izo ndipo akudya izo. Bambo uyu anati . . . Ake—osonkhana ake anapita kwa iye; iye anati, “Chimene ine ndachidalitsa ndi chodalitsika.” Tsopano, kodi icho si chimene wansembe amanena, iye “ali ndi mphamvu yobwezera izo ku thupi la Khristu”? Mwaona, basi sikisi ya chimodzi ndi theka la dazeni la enawo, mofanana basi.

174 Ndipo iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake.” Iye ankayesera kuti ayizembe nkhani ija ya ubatizo mu Dzina la Yesu, chifukwa uyu ndi munthu amene ananena kuti anali—anali wotsutsakhristu amene anachita zimenezo. Iye anati, “Kodi inu mukuganiza kuti ndi zofunikira zonsezo kuti munthu azibatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

175 Iye anati, "Iye atabatizidwa mu dzina la 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera'?"

176 Ine ndinati, "Inde, bwana. Iye sanabatizidwe, nkomwe. Mukuona? Iye sanabatizidwe, nkomwe; palibepo Dzina. Umenewo ndi udindo." Ine ndinati, "Izo sizikuzindikiridwa." Ine ndinati, "Chifukwa chiyani—chifukwa chiyani Petro . . . "

177 Iye anati, "Chabwino, tsopano, ndiloleni ine ndikuwuzeni inu chinachake." Iye anati, "Tsopano, mu Machitidwe 10:49, iye anati, 'Pamene Petro anali kuyankhula mawu awa, Mzimu Woyera unawagwera iwo.'"

178 "Koma," ine ndinati, "iye anapotoloka ndipo anati, 'Kodi munthu angaletse madzi kuti awa asabatizidwe?'"

179 Iye anati, "Chabwino, inu mumayankhula uko, kanthawi kapitako, za Machitidwe 19, kumene Paulo anadutsa ku magombe a kumtunda kwa Efeso, anawapeza ophunzira amenewo." Ndipo anati, "Chifukwa chiyani," anati, "iwo sanabatizidwe mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera."

180 Ine ndinati, "Ayi, iwo anabatizidwa 'kuloza ku kulapa,' osati ku chikhululukiro cha machimo. 'Kuloza ku kulapa,' chifukwa Yesu anali asanadziwikebe. Nsembe inali isanaphedwebe."

Iye anati, "Chabwino, nchifukwa chiyani iwo ankayenera kuti abatizidwenso?"

181 Ine ndinati, "Munthu amene anali ndi mafungulo, ananena izi, 'Pakuti mulole chidziwike kwa inu kuti palibe Dzina lina pansi pa Kumwamba lopatsidwa kwa anthu, limene mukuyenera kupulumutsidwa nalo.'"

182 Chipulumutso chokha chimapita mu Dzina la Yesu Khristu. "Chirichonse chimene muchita mmawu kapena mu ntchito, muchite zonsezo mu Dzina la Yesu Khristu." Palibepo dzina lina, palibe mpingo, palibe ulamuliro wolowezana, palibe maudindo, kapena china chirichonse! Komabe, Iye ndi Duwa la Sharoni, Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa, Alfa, Omega, Woyamba ndi Wotsiriza, Yehova-yire, -rafa, -manasse, zonsezi. Iye ali zinthu zonsezi, komabe Iye . . . Mulibe chipulumutso mu aliwonse a maudindo amenewo; *Yehova,* mulibe chipulumutso; *Duwa la Sharoni,* komabe Iye ali, mulibe chipulumutso; *Atate, Mwana,* kapena *Mzimu Woyera,* mulibe chipulumutso. Kokha Dzina la "Yesu Khristu!" Ndipo kenako Baibulo linanena, kuti, "Kulapa ndi kukhululukidwa kwa tchimo ziyenera kuphunzitsidwa mu Dzina Lake, kuyambira ku Yerusalemu, ndi ku malekezero a dziko lapansi."

Iye anati, "Kodi inu mukuganiza kuti izo zikupanga kusiyana kulikonse?"

183 Ine ndinati, "Bwana, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake." Iye ndi ine, ndi mkazi wanga, tinali titakhala pa tebulo. Iye anangosunthirapo. Anandiwona ine, ndinapita . . . Ine

ndinati, "Ife awiri tonsefe ndi aku Arizona; timakhala kuno. Ndipo ine, ndipo ife tikudziwa khonsolo yathu, ndi dera lathu, ndi onse, ndi ameya athu, kazembe, chirichonse."

Iye anati, "Inde."

184 Ine ndinati, "Tsopano, ngati ine ndikanakuuzani inu, m'bale, kuti, 'Pitani cha kuno ndipo mukasainire chakudya chathu chamadzulo, mu dzina la Kazembe wa Boma la Arizona,' kodi inu mungapite kukasaina izo monga choncho? Kodi inu mukuganiza kuti angakalandire izo pa desiki?"

185 "Chifukwa chiyani," iye anati, "ndikuganiza ayi." Iye anati, "Nchifukwa chiyani Yesu ananena zimenezo?"

186 Ine ndinati, "Izi ndi zimenezo, mwaona. Chifukwa chiyani? Ngati nditakuwuzani inu kuti 'mupite mukasainire chakudya ichi, mu dzina la Kazembe wa Boma la Arizona,' ndipo ife pokhala mbadwa za Arizona, ndipo tikudziwa yemwe Kazembeyo ali, bwanji, inu mungadziwe kuti musaine izo mu dzina la 'Sam Goddard,' mwaona." Ine ndinati, "Chifukwa, iye ndi Kazembe wa deralo. Ine sindikusowa kuti ndikufunseni inu. Inu mukudziwa yemwe Kazembeyo ali. Ndipo, pamene Iye anati, 'Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,' Iye ankadziwa momwe iwo akanabatizira. Iwo ankadziwa Yemwe Iye anali. 'Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa.' Mukuona? Mukuona?"

Iye anati, "Oh, ine ndawona."

187 Koma tsopano, chinthu chotsatira, kodi inu mukhulupirira? Mukuona? "Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo wosatha." Ndipo pamene Moyo Wamuyaya watsopano uwu ukhala mwa inu, Iwo ndi chikole.

188 Pamene inu mwalandira Mzimu Woyera uwu tsopano, zimene iwo anachita pa Pentekoste; iwo anali zimango, tsopano Zimphamvu zimayenera kuti zibwere. Iwo anali atakhulupirira. Inu mukudziwa, amzathu abwino Achibaptisti amatiuza ife, "Pamene ife tikhulupirira, ife tawulandira Iwo." Koma, iwo analibe Iwo, komabe iwo anali atakhulupirira.

189 Machitidwe 19, iwo anali atakhulupirira, koma iwo analibe Iwo. "Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuyambira pamene munakhulupirira?" Mukuona? Iwo anali ndi Zimango, zabwino bwino, chifukwa atumwiwo anali… Kapena, ine ndikutanthauza, Apollo ankaphunzitsa kwa iwo ndi kutsimikizira mwa Baibulo, Zimango, kuti Yesu anali Khristu, koma iwo analibe Zimphamvu apobe. Mukuona? Ndi zimenezotu. Chabwino.

190 [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]…-mango, mwakuyankhula kwina muli nacho chikole, mukudikirira.

191 Tsopano, pamene inu mupeza Zimphamvu, inu mwafulumizitsidwa kuchoka kuchivundi kupita ku

kuchisavundi. Izo zimapangitsa thupi lonselo kumvera Mawu. Izo zidzakupangitsani inu kuchita mosinthika, kuwoneka mosinthika, kukhala mosinthika. Zidzangokupangani inu kukhala wosinthika.

192 Tsopano tayang'anani . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . mwafulumizitsidwa. "Inu amene nthawiyina munali akufa mu tchimo ndi zolakwa, ndi mdima, Iye wakufulumizitsani." Ndi chiyani? "Mzimu Wake umene unamuwukitsa Yesu," mmawa wa Isitala, "kwa akufa. Ndipo ngati Iwo ukhala mmatupi anu achivundi," tsopano penyani, "Iwo udzafulumizitsanso, kubweretsa ku Moyo, kuwapangitsa iwo kuti azimvera Mawu."

193 Tsopano, inu mungadzinenere bwanji kuti muli ndi Mzimu umenewo, ndi kudziponya nokha kutali ndi Mawu? Inu mwafulumizitsidwa ndi chinachake. Pakuti, Iwo udzafulumizitsira matupi anu achivundi ku Mawu. Ndithudi, Iwo udzatero.

194 Inu simungathamange wopanda Iwo. Inu muzingokhavula, ngati inu simukhulupirira zonse za Iwo. Ngati mungokhala ndi chidutswa cha mafuta ndi chidutswa cha madzi, inu simupita kulikonse. Mukuona? Inu mukuyenera kutenga wani handiredi peresenti, mafuta. Ngati simutero, inu muzingophulika, ndipo mulibe mphamvu. Mukuona? "Koma ine—ine ndimakhulupirira *ichi,* koma ine sindimakhulupirira *Icho*," pompu-pompu-pompu. Inu simukupita kulikonse.

195 Koma, oh, pamene inu mutenga chidzalo! Kulola icho chiwalitsire pa izo, Mawu aliwonse ndi Choonadi!

196 Ndiye zindikirani tsopano, pamene ife tikutseka, zindikirani izi. Zindikirani, izo ziri ngati yaying'ono—mbewu yaying'ono ikakhala mu nthaka.

197 Tsopano, mwakuyankhula kwina, inu mwawukitsidwa. Mumawukitsidwa pamene mulandira Mzimu Woyera mwa inu. Inu mumawukitsidwa pomwe apo. Thupi lanulo mwakuyankhula kwina lawukitsidwa.

198 Muyang'ane pa mbewu yaying'ono. Ibzaleni iyo mu nthaka. Iyo ikuyenera kuti imwe kuchokera mu kasupe Wake, madzi amene atsanuliridwa pansi. Ndipo pamene iyo ikumwa, iyo imakankhira mmwamba kwa Iye, ikubwera mochuluka monga chifaniziro cha mbewu imene inapita mu nthaka. Mukuona?

199 Mpingo umabwera mwanjira imeneyo, kudutsa kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, tsopano mu kuphukira. Mukuona? Mzimu wa Mulungu unabwera kudutsa mu zimenezo.

200 Ndipo mzimu wa mdziko wabwera kudutsa mwa wotsutsakhristu, mwanjira yomweyo, ndipo tsopano

ukuphukira mu chilumikizano chachikulu cha mipingo, mwaona, chinthu chonsecho.

201 Ndipo munthu payekha amabwera mwanjira imeneyo. Chirichonse chimagwira ntchito mofanana, pa muyeso womwewo wa Mulungu, chifukwa Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Zindikirani, panjira yanu, mukukula kupita ku chidzalo cha chiwukitsiro, motsogozedwa ndi Mzimu!

202 Pamene dzuwa, d-z-u-w-a, likukoka chomera chaching'ono icho chimene chikumwa kuchokera ku kasupe wa Mulungu, kumangopitirirabe. . . Mwaona, iko kakhoza kungomwa kuchokera ku chinthu chimodzi. Inu mukadzathira mafuta pa mbewu yaying'onoyo nthawi yina; mudzaipha iyo. Izo nzoona. Inu mukathira madzi achithaphwi, madzi akale amene si abwino, iwo ndi ovunda, iwo adzalepheretsa zomerazo. Iyo siyidzabereka chipatso. Nkulondola uko? Koma mukathira madzi abwino kwenikweni amvula ofewa, ameni, opanda mankhwala opangidwa ndi anthu mmenemo, kungowalola iwo abwere kuchokera kumwamba, ndipo mudzapenye chomera chaching'ono icho. Palibe madzi amene angameretse icho ngati madzi amvula aja. Inu mukayika klorini ndi zinthu mmenemo, monga momwe inu mumayesera kutilengula ife, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye amapha chomeracho.

203 Ndiro limene liri vuto lero. Iwo amayesetsa kuwapatsa iwo madzi ochokera ku kasupe wachipembedzo, ndipo iwo amapinimbitsa kukula. Mukuona? Koma mulole iye akhale ndi:

> Bwerani komwe mame achifundo akuwala;
> Kuwale mondizungulira ine usana ndi usiku,
> Yesu, Kuwala kwa mdziko.

Ndiye inu mwachipeza icho, pamenepo.

> Tidzayenda mu Kuwala, kuwala kokongolako,
> Kumabwera kumene mame achifundo akuwala;
> Kungowala mondizungulira ine!

204 Chotsani akasupe opangidwa ndi anthu awa kwa ine! "Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa, palibe koma Magazi a Yesu!" Ameneyo ndi Kasupe yense amene ine ndikufuna kuti ndimudziwe. Mulole Mawu akhale mwa ine, Ambuye; mudziwathirira Iwo ndi Mzimu Wanu.

205 Zindikirani, tsopano, ngati Mzimu umenewo umene unamuwukitsa Yesu kuchoka mmanda, ukhala mwa inu, mwakuyankhula kwina muli nawo Moyo; kumatsogozedwa ndi Mzimu, kukafulumizitsa Mawu kwa inu, kuti muwakhulupirire Iwo. Kanthu kakang'onoko kamapitirira kumakankha pamene iko kakukula.

206 Zindikirani, pa Pentekoste, matupi awo anafulumizitsidwira ku Moyo watsopano. Tayang'anani pa gulu la amantha aang'ono.

207 Kodi ine ndikukusungani inu motalika kwambiri? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Taonani, ine ndangotenthedwa, ndi zimenezo, ndikumverera bwino. Oh, mai!

208 Zindikirani, iwo anali amantha. Zindikirani. Koma, iwo anali ndi Zimango. Mukuona? Koma iwo onse anali atakhala kumbuyo uko, akuti, "Oh, ine ndikuwawopa iwo. Oh, ine ndikuwopa kuti ndipite kunja uko ndi kukadzinenera, chifukwa, oh, mabishopu aakulu onse amenewo ndi zinthu kunja uko. Oh, ine ndikuwopa kutero. Ansembe amenewo ndi zinthu, ine ndikuwopa kuti ndidzinenere zimenezo, ndikuwopa kuti ndikanena kuti ndimakhulupirira pa Iye. Oh, ine basi sindingachite zimenezo, inu mwaona."

209 Koma, zonse mwadzidzidzi, Zimphamvu zinabwera. Inde. Ndipo kodi Izo zinachita chiyani? Izo sizinangodzaza mzimu wawo, mkatimo, koma Izo zinafulumizitsa zimango zawo. Matupi awo anafulumizitsidwa. Iwo sanalinso amantha. Iwo anapita kumeneko pamaso pa anthu. Inde, bwana. "Amuna inu aku Yudeya, ndi inu okhala mu Yerusalemu!" Kumene, Zimphamvu zisanabwere, iwo anangokhala zimango chabe. Mukuona? "Amuna inu okhala mu Yerusalemu, mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani mawu anga! Awa sanaledzere, monga inu mukuganizira."

210 Ndine mmodzi wa iwo. *Ichi* ndi Chija! Ndikuwonetsani inu chimene icho chiri. Ndi Lemba. *Ichi* ndi Chija! Ndipo nthawizonse ndakhala ndikunena, "Ngati *ichi* sichiri Icho, ndiroleni ine ndisunge *ichi* mpaka Icho chitadzabwera."

211 "Ayi, ichi ndi Chijachi chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli, 'ndipo zidzafika pochitika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse.'" Mwaona, Zimphamvu zikubwera mu zimango. Iwo sanachitenso mantha.

212 Ena a anthu inu amene mumawopa kuti mkazi wina akusekani chifukwa chokhala ndi tsitsi lalitali, kapena mwasiya kuzipentapenta; ena a inu amuna amene mukuopa kuti bungwe lanu likuponyerani kunja pamene mubatiza mpingo wanu mu ubatizo wa Mwamalemba; inu mukuyenera kudzitsekera nokha mu chipinda chapamwamba mpaka Zimphamvu zitabwera. Uko nkulondola.

213 Izo zinawasintha iwo. Izo zinawafulumizitsa iwo. Izo zinawapangitsa iwo kukhala osinthika. Iwo anali anthu osinthika, kuyambira pamenepo mpaka. Izo zinawafulumizitsa iwo, kuchokera ku moyo wakale wokhala wamantha, kupita kokhala ngati Mkango wa fuko la Yuda. Iwo mwamtheradi anayang'anizana ndi kufera chikhulupiriro, anakhomeredwa pa mitanda, anapachikidwa chadodolido, anawotchedwa, anaponyedwa mu khola la mikango. Panalibenso mantha, za

iwo. Imfa inalibe chigonjetso pa iwo, nkomwe. Zimphamvu zinali mu zimango. Inde, bwana. Izo zinafulumizitsa thupi lawo lachivundi.

214 Tsopano mvetserani. Apa pali chinthu china, chotsimikizira. Izo zinawafulumizitsa iwo mwanjira imeneyo mpaka (Inu mukudziwa chiyani?) iwo anakwezedwera mmwamba mmalo Ammwambamwamba, ndipo matupi awo achivundi anafulumizitsidwa kwambiri mpaka chinenero chawo chinasintha. Izo basi. . . Izo zinafulumizitsa chinenero chawo. Ndi zimene Baibulo linanena. Ndipo, matupi awo achivundi anafulumizitsidwa, chinenero chawo chinafulumizitsidwa. Malingaliro awo anafulumizitsidwa. Mizimu yawo inafulumizitsidwa. Moyo wawo unafulumizitsidwa. Iwo anafulumizitsidwa, pamodzi! Iwo anayesetsa kuti ayankhule, ndipo sanathe kuyankhula mu zinenero zirizonse za anthu. Iwo anafulumizitsidwa kwambiri mu Kukhalapo kwa Mulungu mpaka iwo anayankhula mu lirime latsopano, chinenero Chakumwamba. Psyii! Ndi Mphamvu yofulumizitsa bwanji!

215 "Ngati Mzimu umene unamuwukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu," oh, aleluya, "Iwo udzafulumizitsa thupi lanu lachivundi." Iwo udzakupangitsani inu kuchita zinthu zimene simunachitepo nkale. Iwo anali odzazidwa ndi Mphamvu yofulumizitsa pamenepo. Mukuona?

216 Thupi lanu silogonjeranso kwa tchimo; inu, zokhumba zanu.

Iye akati, "Bwera kunja kuno!"

Inu mumati, "Tseka pakamwa pako."

"Oh, ife tiri ndi chachikulu kwambiri. . . "

"Tseka pakamwa pako." Mai, ndinu mphungu!

217 Kodi inu munayamba mwawonapo momwe mphungu yakale imayendera payokha? Iyo siyimakupiza ngati khungubwe, mwaona, kupita kwa chakufa chirichonse, ndi zovunda zonse ziri pansi. Ayi, bwana. Iyo imayenda monyadira.

"Tseka pakamwa pako."

"Oh, apa pali chakudya chabwino chamadzulo *kuno*."

218 "Osati za ine. Mwaona, zokhumba zanga zasintha. Chilakolako changa ndi chosinthika. 'Pakuti munthu sadzakhala moyo ndi zovunda za dziko lapansi zokha, koma ndi Mawu onse otuluka kuchokera m'kamwa ya Mulungu.'" Mphungu yeniyeni yofulumizitsidwa imakhala moyo ndi Iwo. Ameni!

219 Oh, ndipo Iye anamuwukitsa Khristu kuchokera mmanda, akukhala mwa inu, wafulumizitsa thupi lanu lachivundi kupita mu Kukhalapo Kwake. Inu mwawazindikira Iwo. Inu simulinso khwangwala. Inu ndi mphungu. Inu simukufuna zinthu za mdziko. Ndinu mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu.

Mukuchita phwando pa Kasupe amene dziko silidziwa kanthu za iye. Inu mukumwa Iye. Winawake akudziwa. . . Dziko silikudziwa kanthu za izo. Inu mukudya Manna obisika amene dziko silinadziwe nkomwe kalikonse za Iwo, pakuti ndinu mphungu. Inu mwafulumizitsidwa pamwamba pamene inu mungakhoze kufika kwa Iwo. Inu simungafike kwa Iwo pansi *apa,* inu mukuyenera kukwera pamwamba *apa.* Inu mukuyenera kuti mufulumizitsidwe, mukwezedwere pamwambapo, kuti Iwo afulumizitse.

220 Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anayankhula mu chinenero china. Baibulo linati iwo anatero. "Iwo anayankhula mu lirime lirilonse pansi pa Kumwamba."

221 Kodi inu mungalingalire zimenezo, matupi akale achivundi amenewo amene ali mmenemo, akuti, "Chabwino, ine sindikudziwa, tsopano, ngati ine ndingakhulupirire izi kapena ayi"?

222 Zonse mwakamodzi, iwo anafulumizitsidwa kwambiri mpaka kulimba mtima kwa Mkango wa fuko la Yuda kunagwera mwa iwo, pamwamba pa Mtolo woweyula uwo. Oh, Mphungu ija inabwera kudzayitana Ake Omwe! "Ndipo iwo sanaikonde miyoyo yawo kufikira imfa." Ameni.

Ndipo padzakhala enanso amene adzapereke
magazi a moyo wawo
Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu
ndi kusefukira Kwake kofiira.

223 Ndipo Mwana akuyenera kuti—adzawululidwenso kachiwiri, mwa Mkwatibwi mu tsiku lotsiriza; Mphamvu yofulumizitsa ikuyenera kuti idzabwere, kudzawafulumizitsa iwo kuchoka mu zipembedzo zakufa izi ndi tizikhulupiriro, kupita ku Mawu amoyo a Mulungu wamoyo. Oh!

224 Ayi, Iyo inawafulumizitsira iwo ku Moyo watsopano. Iyo ikuchita chinthu chomwecho kwa ife tsopano. Zindikirani, ndiye, iwo anafulumizitsidwa kwambiri mu Mphamvu yofulumizitsa imeneyo! Tsopano ine. . .

Mvetserani mwatcheru tsopano. Ine ndikuyesetsa kuti ndikuwonetseni inu.

225 Mphamvu yofulumizitsa siinali kokha mu moyo wawo, koma Iyo inali ponseponse pa iwo. Iwo. . . Si Zimphamvu zokha zinabwera, kudzafulumizitsa, koma Izo zinafulumizitsa zimango. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iwo anafulumizitsidwa kwambiri mpaka malirime awo anayamba kuyankhula mu chinenero china. Iwo anafulumizitsidwa kwambiri ndi Mphamvu ya chiwukitsiro cha Khristu, mpaka iwo amayika manja awo. . . Iwo anafulumizitsidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa, mpaka, pamene iwo anayika manja awo pa odwala, iwo anachira. "Iyo inafulumizitsa thupi lanu lachivundi." Iwo anachiritsidwa, posanjika dzanja lawo.

226 Ndipo Mzimu unafulumizitsa chiyanjano chawo limodzi ndi Mulungu, mpaka iwo nawonso anafulumizitsidwa kwambiri mu Kukhalapo kwa Mulungu mpaka, pamene munthu anafa ndipo solo yawo inachokapo, Iwo unamubwezeretsa ku moyo kachiwiri. Ameni! Ulemelero! Tsopano ndikumverera mwachipembedzo.

227 Uko nkulondola, anafulumizitsidwa! Osati kokha chiwukitsiro Chake chinali cha Iyemwini, koma kwa aliyense yemwe angafune, kwa Mbewu yokonzedweratu iyi yomwe ili pamenepo. Kufulumizitsa, kufulumizitsa thupi lachivundi!

228 Iwo anayika manja pa odwala; iwo anachira. Iwo anapemphera; mu Mzimu iwo anawona masomphenya, anayitanira akufa kuti akhalenso moyo. Izo nzoona. "Anafulumizitsa matupi awo achivundi."

229 Ngati Iwo ubwera mwa inu; ngati zikhala chomwecho... Tsopano, inu mukhoza kunena kuti ziri choncho; koma ngati izo ziri choncho, zizindikiro izi zimatsatira izo, inu mwaona. "Iwo umafulumizitsa thupi lanu lachivundi." Iwo udzakufulumizitsani inu.

230 Tsopano, zindikirani, kufulumizitsira mu Kukhalapo kwa Mulungu. Bwanji? Iwo unali Mzimu wa Mulungu umene unamuwukitsa Yesu kuchoka mmanda. Ndipo, Mzimu wa Mulungu, "Ine ndikupereka kwa iwo Moyo Wamuyaya," zimachokera ku mawu Achigriki, ngati mungawayang'ane iwo, *Zoe*, chimene chimawusunthira Iwo kudutsa mwa inu ndipo kenako nkufulumizitsa (awo) ngakhale malingaliro awo.

231 Tsopano penyani. Inu munganene bwanji kuti Mzimu umenewo ukukhala mwa inu? Ngakhale inu mwachita chirichonse chimene inu mukuganiza kuti chinali cholondola, nawu umboni wanu ngati inu muli nawo Iwo kapena ayi. Ngati Mzimu umene unali mwa Khristu uli mwa inu, Iwo udzakufulumizitsaninso inu ku Mawu, pakuti Iye ndi Mawu. Ndipo ngati izo, mosiyana, ukufulumizitsani inu kutali ndi Mawu, ndiye si Mzimu wa Khristu! ...kusamala chimene inu mwachita, mpaka Iwo utakusunthirani inu mu Mawu. "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa, ndipo izo zidzakhala moyo ndi Mawu aliwonse," Mawu aliwonse! Ine ndimayankhula pa izo tsiku lina.

232 Amayi anga omwe, iwo anatsogola tsopano, ndipo iwo anali mkazi wosamvetseka kwambiri. Ndipo iwo anali, inu mukudziwa, pafupifupi theka Mmwenye, ndipo iwo anali osamvetseka. Koma mmenemo anali munthu amene sankalota. Koma ine sindikuganiza...Iwo anali ndi maloto foro kapena faivi okha, moyo wawo wonse. Koma nthawi zonse akalota loto, ilo limakhala lowona. Iwo anali ndi loto, ilo linali lowona.

233 Ine ndikukumbukira nthawi yina pamene ndinayamba kulalikira, zaka zambiri zapitazo. Ife tinkakhala komwe kuno

pa msewu, basi chakumtunda kuno. Ine ndinali kulalikira pomwe pano pa tchalitchi chino. Ndipo iwo analota loto, kuti ine ndinali nditayima apa pambali pa masitepe atatu. Ndipo ine ndinali nditayima, ndikulalikira kwa aliyense, kuti iwo akuyenera kuyenda masitepe atatu awa iwo asanafike pa msewu wawukulu. Ndipo mumsewu waukulu munali mzere woyera wonga ngale, wolowera molunjika ku—ku—zitseko za Kumwamba, ku chipata cha ngale. Ndipo ngaleyo inali itatambasulidwa pamwamba pa masitepe awa. Ngati uwo si Uthenga wanga ndendende lero: kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera! Ndipo ine ndinali kunena kuti munthu ayenera kubwera ndi masitepe atatu awa, kuti athe kuyenda mumsewu waukulu umenewo. Ndipo ananena kuti . . .

234 Panali dona wina amene anabwera. Tsopano, inu mukudziwa mtundu wa nsapato zimene anthu ankavala zaka sarte faivi zapitazo. Panali dona anabwera, anali atavala peyala yaikulu kwambiri monga iwo amavalira lero, nsapato za zidendene za nsonga. Ndipo iye anabwera. Ndipo ine ndinati, "Dikirani miniti, mlongo. Inu simungakhoze kuyenda mumsewu waukulu umenewo ndi izo." Ndipo ine ndinati, "Inu—inu, inu simungachite zimenezo."

235 Ndipo iye anati, "Ah!" Iye anati, anayang'ana pamenepo pa akazi ena onsewo, anati, "Musamukhulupirire iye. Iye ndi wamisala. Mukuona? Musamukhulupirire iye. Ine ndikuwonetsani inu kuti ine ndikhoza kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi kumayendabe ndi zimenezo." Ndipo iye . . . Ine ndinangomusiya iye azipita. Sindikanachita zochuluka za izo, sindikanakhoza kumuletsa iye. Ndipo iye analumphira mmwamba pa msewuwaukuluwo. Ndipo anayang'ana mmbuyo kwa mlongoyo, anati, "Mwaona, ine ndinakuwuzani inu!" Iye anayamba kuthamangira chokera, ndipo iye . . .

236 Inu mukudziwa, monga Baibulo linanena, mu Yesaya, mutu wa 5, kuti iwo akanadzakhala ndi "makosi otambasuka." Iwo akuyenera kutero; iwo asomekedwa, mwaona. "Kunyang'ama pamene . . ." Iwo akuyenera kutero, akuyenera kupotoza, "Kunyang'ama pamene akupita, akudzigwedeza ndi zidendene zawozo; mwaona, ana aakazi a Zioni mu tsiku lotsiriza."

237 Ndipo iye ananyamuka kupita mu msewuwaukulu umenewo, mwamphamvu basi momwe iye akanathamangira. Ndipo, patapita kanthawi, msewuwo unayamba kucheperachepera. Iye anayamba kuphepheluka, akunyang'ama monga *choncho*, ndipo kumbali iye anapita.

238 Ndipo amayi anati, "Kukuwa koyipitsitsa kumene ine ndinayamba ndakumvapo mmoyo wanga, anali mkazi ameneyo akugwera mu malawi amenewo ndi utsi, akupita pansi, pansi

monga choncho." Anati, ine "ndinapotoloka ndipo ndinati, 'Mukuona?'"

239 Iye anangomvera chirichonse kupatula Mawu amodzi, mwaona, chirichonse kupatula Mawu amodzi. Ndithudi, akazi Achipentekoste akhoza kupulumutsidwa, kuyeretsedwa, ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo kenako nkulephera. Mwamtheradi. "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse amene atuluka." Mukuona? Mukuona? Ndipo iye anawalephera Iwo. Ndipo monga ine ndinanena, mwaona, iye akanalowako, bwino bwino, koma, mwaona, iye analephera kuti amvetsere; ndikumuwuza iye chimene chinali patsogolo. Ndipo Iye analemba Uthenga ndi ophunzira, atumwi, ndi Chiphunzitso cha atumwi ndi aneneri, ndi zina zotero, ndipo iwo samamvera.

240 Tsopano zindikirani Mphamvu yofulumizitsa iyi, *Zoe*, kubweretsa Mawu, malingaliro amene anali mwa Khristu anali mwa inu pamenepo. Ine ndikuyesetsa kuti ndikuwonetseni inu, kuti, inu, pamene munawuka. Pamene Mulungu anamuwukitsa Yesu kwa akufa, Iye anakuwukitsani inu, inunso. Ndiponso munafulumizitsidwa ku Moyo, ndi Iye, inu tsopano mwafulumizitsidwa ku Moyo, ngakhale pamenepo inu munali chabe chikhumbo mu malingaliro Ake, koma Mulungu anali atawona zonse mwa Iye, pa mapeto, mwaona. Pamene Mulungu anayang'ana pansi pa thupi . . .

241 Mzimu unamuchokera Iye, Mmunda wa Getsemane. Iye ankayenera kuti afe, munthu. Kumbukirani, abwenzi, Iye sankayenera kuti achite zimenezo. Ameneyo anali Mulungu. Mulungu anadzoza mnofu umenewo, umene unali mnofu wa munthu. Ndipo Iye sanatero . . . Ngati Iye akanapita kumeneko, ngati Mulungu, Iye sakanafa imfa ya mtundu umenewo; sangakhoze kumupha Mulungu. Koma Iye sankayenera kuti achite zimenezo.

242 Koma, kumbukirani, Iye anapita kumeneko ali ndi inu mwa Iye. Mwaona, Mulungu anali asanamulekanitse Mkwatibwi kwa Mkwati, apobe. Chotero pamene Mulungu anayang'ana pansi pa thupi la Khristu, Iye anawona awiri onse mwamuna ndi mkazi. Izo zonse zinawomboledwa mu thupi limodzi limenelo. Mukuona? Iwo ndi mmodzi, ofanana, Mawu omwewo. Mawu omwewo, amene anayankhula za Mkwati, akuyankhula za Mkwatibwi.

243 Chabwino, Mkwatibwi angakhoze bwanji kubwera, ndipo nkulephera kuwonetsera chirichonse chimene chinalonjezedwa za Iye; ndipo Mkwati nkubwera, ndipo Iye osakhala Mkwatibwi? Koma pamene Iye anachita chirichonse, ngakhale kutsimikizira izo podziwukitsa Yekha kwa akufa, mtsogolo mwake, ndiye kodi a—Mkwatibwi sakuyenera kuti achite chinthu chomwecho, ayenera kukhala ndendende chomwe Mawu anati

Iye akanadzakhala mmasiku otsiriza ano? Kodi Iye sakuyenera kuti abwerere kupyolera mu Malaki 4? Kodi Iye sakuyenera kuti awonetseredwe monga izo zinali mmasiku a Sodomu? Kodi dziko silikuyenera kuti likhale chimodzimodzi basi monga momwe liriri? Kodi zinthu izi si chizindikiritso changwiro cha Mawu a Mulungu odziwika kwa ife?

244 Chabwino, abwenzi, ine ndikudziwa kuti ndikukusungani inu nthawi yayitali, maminiti fifitini kuti ifike nthawi ya chakudya chamadzulo, koma mwinamwake ndikhala nditamaliza pofika nthawi imeneyo. Koma zindikirani, taonani apa, ndi chinthu changwiro bwanji chomwe icho chiri. Ine sindikudziwa kuti ndidzakuwonaninso inu liti. Mukuona?

245 Taonani, zindikirani ichi. Koma Mulungu anamuwoneratu Mkwatibwi mwa Mkwati. Aleluya! Mwaona, kuti adzamupulumutse Mkazi Wake, monga Adamu, Iye ankayenera kuti apite ndi Iye. Adamu ankadziwa chimene iye anali kuchita; Eva sankadziwa chimene iye anali kuchita, koma Adamu anatuluka ndi mkazi wake. Mukuona? Ndipo Yesu anatenga malo a Mkazi Wake ndipo anadzakhala tchimo chifukwa cha Iye. Kumbukirani, Iye anadzakhala inu, Iye anayimira chilango chanu, kuti inu mudzakhoze kuyima mmalo Mwake. Iye anaima mmalo mwanu, kuti inu mudzayime mmalo Mwake. Ndi chikondi chotani! Ndi chiyanjano chotani! Ife tingazikane bwanji zimenezo? Ife tingakhoze bwanji kuchita chirichonse kupatula kumukonda Iye, mzanga? Ine ndikhoza kukhala pa izo maora, koma tiyeni tipitirire patsogolo pang'ono.

246 Monga chochitika cha chipentekoste lero, ndi kudza kwa Mzimu Woyera mmasiku otsiriza ano, monga zinalonjezedwa, ziri ngati mtheradi ku chikalata cha umwini. Mukuona?

247 Tsopano, mukhoza kupeza chikalata. Ndithudi. Mukuona? Mukhoza kupeza chikalata cha malo, koma izo sizikunenabe kuti ndi anu. Ayi, bwana. Winawake kumbuyo akhoza kudzabwera ndi kudzanena kuti iwo ndi ake. Koma pamene inu mupeza mtheradi, izo zimawonetsera kuti chirichonse chimene chimatsutsa konse izo chachotsedwapo, mmbuyo momwe kuchokera ku maziko. Nkulondola uko?

248 Ndipo pamene munthu wanena kuti iye akukhulupirira Mawu, ndipo kenako pamene Mzimu Woyera wabwera, Iwo ndi mtheradi ku chikalatacho. Ndipo izo zimakupatsani inu chilolezo, pamene mukhala ndi mtheradi umenewo, kuti gawo lirilonse la izo ndi lanu, ndipo chirichonse chimene chiri pa izo ndi chanu. Ameni! Ndipo izo zimatipatsa ife mtheradi, pamene Mzimu Woyera ubwera pa chikalata chaumwini ichi chimene Mulungu anachiwona mmbuyo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, ndi kuyika dzina pa Bukhu la Moyo; koma tinabadwa kupyolera mwa mwamuna ndi mkazi, ndipo ogonjera ku tchimo, ndi olakwira tchimo. Koma pamene ndinakhulupirira

pa Iwo, ine ndinalandira chikalatacho; koma pamene Mzimu Woyera unadzabwera, Iwo unali mtheradi kuti chirichonse chonditsutsa ine, kaya amayi anga anachita icho, abambo anga anachita icho, agogo anga aakazi anachita icho . . .

249 Monga mwana wamng'ono, wakhunyu yemwe ndinamupempherera, maminiti angapo apitawo, amene anabwera kuchokera kwa azigogo. Khunyulo linagwera pansi, ndipo pa mwanayo, ine ndinati.

250 Koma pamene mtheradi wabwera, Iwo unadzachotsa, unadzafufuta chirichonse. Ndine mwini wa mtheradi pamenepo. Ameni! Ndipo motsimikiza basi monga Mzimu umene unamuwukitsa Khristu kwa akufa, ine ndiri ndi mtheradi wa chikalata kuti ndine gawo la Thupi limenelo, ndi mtheradi wa Mzimu Woyera kupangitsa thupi limenelo la Mawu kukhala chimodzimodzi basi monga Iwo unachitira mwa Iye, monga Iye analonjezera mu tsiku lotsiriza. Mtheradi! Machimo anga onse achotsedwapo, machimo anu onse achotsedwapo, ndi Mwazi wa Yesu Khristu, ndipo Mzimu Woyera wabwera ngati mtheradi ku chikalata chaumwini chimene Mulungu anandipatsa ine mwa chisomo, mwa kudziwidwiratu. Oh, mai!

251 Kodi inu mukuwopa chiyani? Nzosadabwitsa Iye anati, "Musawope; Ine ndine Iye amene ndinali wakufa ndipo wamoyo kachiwiri; ndipo Ndine wamoyo kosatha; ndipo ndiri nawo mafungulo a imfa ndi hade." Musadandaule za chirichonse. Ngakhale imfa sidzakupwetekani inu. Zindikirani. Zokongola!

Tiyeni tipite mwaliwiro tsopano.

252 Chikalata cha mtheradi! Ngongole yathetsedwa. Chirichonse chotsutsa icho chachotsedwapo. Ha-ha-ha! Ulemelero! Ine ndikhoza kuchita mopusa, koma ine ndikumverera bwino. Zindikirani. Mukuona? Oh, chikalata cha mtheradi, kodi inu mukuzindikira chimene icho chikutanthauza? Kodi inu mukuzindikira chimene icho chikutanthauza, m'bale? Palibe chimene chingachotse icho kwa inu. Ameni. Ndine mwini. Ameni. Chimene a . . .

253 Chikalata chanji? Ine tsopano ndapereka kwa wopindula wanga, za imfa Yake, kuyikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro. Iye anakhala ine, kuti ine ndidzakhoze kukhala Iye. Tsopano, Iye anadzakhala wochimwa, kuti ine ndidzakhoze kukhala mwana, ameni, ndi kukhala ndi chikalata cha mtheradi. "Pakuti zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira," mwaona, chikalata cha mtheradi!

Tsopano mwaliwiro, tisanati . . . Tiri ndi pafupifupi maminiti teni owonjezera.

254 Tiyeni ife tsopano tizindikire, mwamsanga, kufulumizitsa kwa Mzimu. Ine ndikuwonetsani inu zizindikiro zina kuti inu mumvetse. Taonani, tsopano penyani chimene, iyi "Mphamvu yofulumizitsa" inali phunziro langa. Mwana atatha kuwuka,

taonani momwe Iyo inachitira pa iwo pa Pentekoste, chimene Iyo inachita kwa iwo, chimene Mphamvu yofulumizitsa ija inachita kwa iwo. Iyo inawafulumizitsa iwo.

255 Tsopano tiyeni tizindikire chimene Iyo inachita pa Stefano. Stefano anali wodzadza ndi Mphamvu yofulumizitsa. Kodi si kulondola uko? Mwaona, iye anali wodzadza ndi Mphamvu yofulumizitsa. Iyo sinamupangitse iye kuchita mantha. Iye anati, "Inu owuma-makosi ndi osadulidwa mu mtima ndi mmakutu, inu nthawizonse mmawukaniza Mzimu Woyera; monga makolo anu ankachitira, inunso mukutero. Ndi ndani wa mneneri amene anawonetsera kudza kwa Wolungama Uyo, amene makolo anu sanamugende?" Oh, mai! Anachita chinachake kwa iye. Ndithudi, iye anali wodzadza ndi Mphamvu yofulumizitsa.

Ndipo iwo anati, "Ife tithana naye munthu ameneyo!"

256 Ndipo pamene ankafa, iwo anamugenda iye; ndi mutu wake wawung'ono wosauka, miyala ikumenya pa iwo monga choncho. Iye anayang'ana mmwamba ndi kuti, "Ine ndikuwona Mmiyamba mutatseguka." Mphamvu Yofulumizitsa inali ikugwira ntchito. "Ine ndikuwona Mmiyamba mutatseguka, ndipo Yesu atayima pa dzanja lamanja la Mulungu." Ndicho chimene Mphamvu yofulumizitsa inachita kwa Stefano.

257 Zindikirani munthu wina, anali ndi Mphamvu yofulumizitsa iyi, dzina lake linali Filipo. Iye anali wodzaza kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa. Iye anali ndi msonkhano waukulu wopambana uko ku Samariya. Ziwanda zinali zikutulutsidwa. Anthu ankabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Iwo anali ndi msonkhano weniweni. Ndipo Mzimu unayankhula kwa iye, oh, a—Zimphamvu zinatsika pansi, ndipo Iwo unati, "Siya chitsitsimutso ichi." Koma kodi atumiki adzanena chiyani? Sizikupanga kusiyana kulikonse chimene iwo anganene. Mukuona? Iye anali wodzaza ndi Mphamvu yofulumizitsa. Iye anali ndi mafuta, ndipo—Zimphamvu zinali zikugwera pa iye. Anati, "Pita ku chipululu."

258 Ndipo anakampeza mdindo kumeneko, ndipo anamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu; munthu mmodzi, amene anautengera Uthenga ku Ethiopia. Nkulondola uko? Ndipo iye anamumvera Mulungu.

259 Mu kumvera kwa Mulungu, ngati inu simunabatizidwepo mu Dzina la Yesu Khristu, chitani izo, ndipo mudzawone Mphamvu yofulumizitsa ikukunyamulirani inu mmwamba pamenepo. Mukuona?

260 Pamene Stefano anachita chinthu chachikulu ichi... kapena, osati Stefano. Koma Filipo anachita chinthu chachikulu ichi, kusiya chitsitsimutso chachikulu chimenecho ndi kumvera malamulo a Mulungu, pamene iye anakwaniritsa, mwa kudzaza...Pomubatiza mdindo uyu, mu kumvera kwa Mulungu, iye anali wodzaza kwambiri ndi Mphamvu

yofulumizitsa mpaka Iyo inamutengera iye kutali. “Iyo idzafulumizitsa thupi lanu lachivundi, ngati Mzimu uwu umene unamuwukitsa Yesu kwa akufa.” Iyo inamufulumizitsa Filipo mpaka iye sanawoneke kwa mwinamwake mailosi handirede fifite, cha kwinakwakenso, uko mu dziko lina. Iyo inafulumizitsa thupi lake lachivundi. Kodi iye anachita motani izo? Iye anali wodzadza kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa.

261 Oh, Mpingo wa Mulungu wamoyo, ife sitingayime muzungulira pano kumayamwa timatiti ta shuga tating’ono timene ife tikuyamwa kuno lero. Ife tikuyenera kuti tizikhala okhuta ndipo titapemphera, ndi Mphamvu yofulumizitsa, kufikira ku kufulumizitsa kwa Mzimu Woyera! Ife tikuyenera kuti tidzatengedwere kutali, tsiku lina, mu Mkwatulo umenewo uko. Inde, bwana. Ameni! Oh, mai!

262 Mukhululuke kafotokozedwe kameneko. Ine ndimaganiza za mayi amene amapanga timatumba tating’ono timeneto, ife tinkakonda kutero, ta khanda. Ena a inu amayi akale mukukumbukira zimenezo. Mwana wamng’onoyo akayamba kulira; inu mumatenga njere za khofi ndi shuga pang’ono, mumazikulunga izo mkathumba ndi kumusiya iye aziyamwa izo, kuti zimutonthoze iye. Mulibe mphamvu mu zimenezo. Izo zimupha iye. Mukuona? Kafini wakale uja mmenemo, ndi zinthu, zotsekemera pang’ono kuti zimupangitse iye kumeza izo, zikulowetsa kafini mwa iye.

263 Ife tinatopa nazo zinthu zoterozo ngati izo. Bwererani! Ndinu mphungu; kubwerera ku Mawu a Mulungu! Mukhale amphamvu; palibe chimene chingapweteke kumverera kwanu, chotero ndinu mfulu ku zamanyazi zonse za munthu. Chirichonse chimene aliyense anganene motsutsa inu, icho chimangobweretsa chikondi chochuluka. Ameni. Ndipo, Mphamvu yofulumizitsa, inakwatula kupita Mmwambamwamba, mphungu imene inawuluka pamwamba pa nkhukuzo, kutali uko mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu! Oh!

Iyo inali pa Filipo. Iyo inamufulumizitsa iye, inamutengera iye kutali.

264 Tiyeni timutenge munthu wina. Kunali munthu wina dzina lake Enoki. Tsopano, iye anali atayenda ndi Mawu aliwonse a Mulungu, kwa pafupifupi zaka faivi handirede. Iye anali ndi umboni, wakuti, “Ine sindinalepherepo nthawi imodzi Mawu Ake.” Iye anadzazidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa pamene Zimphamvu zinamufikira iye, pa Zimango zimenezo, iye sankayenera nkomwe kuti afe; iye anangotengedwera mmwamba wa Kwawo. Anangoyamba kuyenda. Iye anali. . . Monga Filipo, iye anali wodzazidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa, mmalo mopita ku Gaza ndi kupita kumalo ena, kumene, iwo anakamupeza iye mmagombe akumtunda

kumeneko. Mmalo mwa njira imeneyo, iye anangopita, oh, anati, “Ndine bambo wokalamba, mulimonse. Ine basi ndiri nayo Mphamvu yofulumizitsa yochuluka kwambiri, ine ndingoyenda kuchoka pa dziko lapansili.”

265 Ndiyo Mphamvu yofulumizitsa yomweyo imene ife tiri nayo pakali pano. Mwaona, Iyo idzafulumizitsa thupi lanu lachivundi. Si kulondola uko? Iyo ndi Mphamvu zofulumizitsa.

266 Enoki, ndi umboni wangwiro umenewo, kuti, “Chirichonse chimene Mulungu anandiuza ine kuti ndichite, ine ndinachichita icho. Chirichonse chimene ine ndinachiwona chimene Iye anandiuza ine kuti ndichite, ine ndinachichita icho.” Ndipo iye anakhala wodzazidwa kwambiri—ndi Zimphamvu, kapena—kapena Zimango, mpaka, pamene Mphamvu yofulumizitsa inamukantha iye, Zimango, Iyo inangomunyamulira iye mmwamba. Iye anayenda kuchoka pa dziko lapansi, kupita Kumwamba.

267 Tsopano, tsopano zindikirani, pa Eliya. Pambuyo. . . Taonani, Eliya, mneneri wamkulu uja, mwamuna mu tsiku lake. Mundikhululukire ine. M’bale, mlongo, mu tsiku limenelo iye anali atawazazira akazi openta nkhope amenewo, ma Yezebeli amenewo ndi ma Ahabu. Ndipo anayima mpaka. . .Ndipo panalibe wina, ankawoneka ngati, anayima ndi iye. Ndipo iye anadzudzula, ndipo anawononga, ndipo anayima kunja uko, ndipo Mulungu anali atamusamalira iye ndi kumuthandizira iye mmalo aliwonse. Inu mukudziwa, munthu wachikulireyo anatopa tsiku lina. Iye anati, “Ine ndikukalamba, chotero sindingathenso kupita patsogolo.” Iye anali akupitirira, ine ndikuganiza, usinkhu wa zaka nainte; atakalamba kwenikweni, ndipo akuyendayenda kumeneko, ndipo iye anali wodzazidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa. Inu mukudziwa chiyani? Iye anayang’ana kutsidya kwa Yordano.

O Mulungu! Ndikutha kuwona mbali inayo. Simukutha inu?

268 Wodzazidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa, mpaka, iye anawona galeta atakolekedwa pamenepo, akavalo a Moto ena ndi galeta la Moto, atakolekedwa ku mtengo wina kumeneko. Iye anangoyenda kuwoloka mtsinjewo ndipo anapita Kwawo, popanda ngakhale kufa. Mphamvu yofulumizitsa inatumiza, inapangitsa galeta kutsika kuchokera Kumwamba ndipo inamunyamulira iye mmwamba. Inanyamula ngakhale chikhoto chake ndi kudzachiponyera icho mmbuyo kwa Eliya. Uko nkulondola.

269 Tsopano, ndiye munthu ameneyo ananyamula mwinjiro umenewo, choyimira Mpingo kachiwiri, mwaona, ananyamula mwinjiro umenewo. Tsopano, iye anachita kawiri zozizwitsa, chimene chiri choyimira Khristu ndi Mpingo. Mukuona? Eliya anachita kanayi; iye anachita kasanu ndi katatu. Mwaona, tsopano, iye anali—iye anali pawiri mphamvuyo, chifukwa

iye anapempha izo. "Zinthu zazikulu zoposa izi zimene Ine ndikuzichita inu mudzazichita." Mukuona? Koma iye anali wodzazidwa kwambiri ndi Mphamvu yofulumizitsa, ndi chirichonse, mpaka iye anachita zonse izi, pawiri, zimene Elisha anachita, kuposa momwe iye anachitira. Ndipo zindikirani, iye anakhala moyo mpaka pafupifupi usinkhu wa zaka eyite kapena nainte, iye anakalamba ndipo iye—iye anafa. Iye anafa, ndipo iwo—iwo anamutenga iye ndi kukamuyika.

270 Inu mukudziwa, chabwino, Mphamvu yofulumizitsayo sinamusiye iye. Zaka zambiri, zambiri zitachitika izo, pamene mnofu wonse unali utavunda kuchoka pa mafupa ake, iye anali ali mmanda. Ndipo iwo anali atanyamula munthu wakufa tsiku lina, ndipo iwo anawona mdani, ndipo anangomuponyera munthu uyu pamwamba pa mafupa a Elisha. Pamenepo panali Mphamvu yofulumizitsa yochuluka kwambiri pa mafupa amenewo mpaka munthuyo analumpha kukhala wamoyo kachiwiri. Oh!

271 "Iyo idzafulumizitsa thupi lanu lachivundi." Ngakhale wakufa ndi wovunda mmanda, ndipo komabe Mphamvu yofulumizitsayo inali pa dothi limenelo. Aleluya! Uh! "Iye amene anawukitsa Khristu kwa akufa adzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi." Eliya kumbuyo uko, Elisha ndi Eliya . . .

272 Kumbukirani, munthu wakufa ameneyo, mneneri ameneyo, wodzazidwa ndi Mphamvu yofulumizitsa imeneyo, ali mmanda ndipo atavunda; mmenemo munali Mphamvu yofulumizitsa yochuluka kwambiri, mpaka, iwo anaponyera munthu wakufa pa iye, iye anakhala moyo. Iye akhozabe kuyika manja pa odwala, sichoncho iye? Ameni. Ndi zimenezotu.

273 Ndipo kumbukirani, ife ndi mnofu wa mnofu Wake, Yesu Khristu. "Ndife mnofu wa mnofu Wake, ndi mafupa a mafupa Ake." Oh, palibe njira yotulukira mu izo. Ife tidzawuka, ndipo ndizo zonse. Inu mudzawuka, ndizo zonse.

274 Isitala imatanthauza zochuluka kuposa mwambo chabe. Izo zirinso tsopano, pakuti matupi athu amafulumizitsidwa ndi Iye ndipo tikukhala mmalo Ammwambamwamba.

275 Ndipo thupi ili likhoza kuvunda mnyanja; likhoza kuvunda mu nthaka; pakhoza osakhala phulusa lodzaza supuni; koma iye akubwera. Pakuti, Mzimu umene unawukitsa Ambuye wanga kwa akufa wafulumizitsa thupi lachivundi ili. Iwo wafulumizitsa thupi lanu lachivundi. Ndipo ife ndi opindula Ake a chiwukitsiro Chake, ndondomeko Yake ya Moyo Wamuyaya imene ine ndimaiyankhula mochuluka za iyo, inu mukudziwa. Nzosadabwitsa Iye anati, "Musawope." Iye akanazadziwa.

276 Pakuti monga Paulo anati, "Imfa, mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Ndine wodzaza ndi Mphamvu yofulumizitsa. Mayamiko akhale kwa Mulungu,

Amene amatipatsa ife chigonjetso mwa Ambuye Yesu Khristu wathu." Inde, bwana! Mphamvu Yofulumizitsa. Oh, mai!

277 Iye ndi wamoyo kwamuyaya, "yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ahebri 13:8. Zindikirani, Mesiya, Mmodzi wodzozedwayo; chomwechonso ali Mkwatibwi Wake, mkazi wa Mesiya, mwaona, Mmodzi wodzozedwayo.

278 Zindikirani, imfa simaimitsa Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu. Imfa singayimitse Iyo. Pamene inu muli nayo Iyo, Iyo ndi Yamuyaya. Palibe chirichonse chimene chingaimitse Iyo. Inu simungakhoze kuiyika pagoli Iyo; simungakhoze—simungakhoze kuchita chirichonse kwa Iyo. Inu muzikhala moyo wanu, izo sizimaimitsabe Iyo; yabwino basi monga momwe Iyo inaliri.

279 Zindikirani, Mose ndi wodzaza ndi Mphamvu yofulumizitsa imeneyo. Kodi iye anali? Iye anali mneneri yemwe Mawu ankafikirako. Iye anali gawo la Mawu. Iye anali Mawu a tsiku limenelo. Nkulondola uko? Ndipo iye atafa, zaka eyiti handirede, pa Phiri la Chiwalitsiro, pamenepo iye anayima, ndi Eliya. Nkulondola uko? Mphamvu yofulumizitsa, imfa siyimaichotsa konse Iyo. Ayi, ayi. "Ine ndidzawukitsa ilo kenanso." Angelo anabwera; anadzamuyika iye kumusi uko mchigwa. Iye anali atavunda ndipo atapita, mafupa ake anali atapita, ndi china chirichonse, koma Mphamvu yofulumizitsa inali ikanali pamenepo. Iyo inamufulumizitsa iye ndi kumudzutsa iye. Ndipo apo iye anali, atayima pamenepo. Zindikirani.

280 Inu mukuti, "Nkulondola uko, M'bale Branham, zitatha zaka eyiti handirede?" Oh, mai!

281 Ngati inu mungawerenge mu Mateyu, ine ndiri ndi Lemba, Mateyu 27:51. Inu mukhoza kulemba, kulemba izo. Pamene onsewo kumbuyo uko, amene ankakhulupirira kuti Iye akanadzabwera. . .Baibulo linanena apa, Iye atabwera, iwo anali akugona mu nthaka. Mphamvu yofulumizitsa inali pa iwo, ndipo iwo anali gawo la Iye, oyera amenewo. Iwo anali gawo la Iye, chifukwa iwo anali atakhulupirira pa Iye.

282 Mwakuyankhula kwina iwo anali ndi Moyo umenewo, kudzera mu nsembe ya nkhosa, chitetezero, imene sikanabweretsa konse mzimu wa nkhosa pa munthu. Nanga bwanji tsopano ndi Mzimu wa Munthu, Mulungu Mwiniwake, pa inu, mwaona, ndi Mphamvu yofulumizitsa yochuluka bwanji imene ife tiri nayo! Koma kupyolera mu chitetezero cha tchimo anaperekedwa mwanawankhosa, mwa choyimira. Chimene tiri nacho sichoyimira; icho ndi choyimira motsutsa. Kodi ife tikuwopa chiyani? Ndipo anthu amenewo amene anali ndi choyimira chokha, cholozera ku chiwukitsiro Chake, ndipo anapita uko mmanda ndi icho.

283 Monga Yobu kumbuyo uko pansi pa kupsyinjika kwake kwakukulu, mai, chirichonse chitachotsedwa kwa iye! Mdierekezi anati, “Ndiroleni ndimutenge iye. Ndimupangitsa iye kuti akutukwaneni Inu pamaso Panu.” Ndipo kenako iye anamasuka.

284 Anati, “Iwe usatenge moyo wake.” Ndipo anachita (iye) zonse kupatula kutenga moyo wake.

285 Ndipo mkazi wake anamutembenukira iye. Anati mpweya wake unali wachilendo kwa iye. Mwakuyankhula kwina, iye—iye alibe chochita ndi iye. Iye sankawoneka kuti amamukondanso iye, anangomukankhira iye kutali. “Yobu, ndiwe womvetsa chisoni! Bwanji osangomutukwana Mulungu, ndi kufa?”

Anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Oh, mai!

286 Mwaona, iye anagwiritsitsa ku chimene iye anali nacho. Tsopano, iye anali mneneri. Iye anati, “Ine sindine wochimwa. Ine ndapereka nsembe yoperekedwa.” Ameni. Iye ankadziwa pamene anali kuyima. Iye anali pa Mawu. Ziribe kanthu chimene enawo ankanena, iye anali pomwepo pa Mawu. Kenako ora lalikulu lopambana lija . . . Anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Iye anati, “Ambuye anapereka, Ambuye watenga; bwanji, lidalitsike Dzina la Ambuye!” Anati, “Ndinabwera mdziko lino wopanda kalikonse. Ine ndinabwera kuno, wamaliseche, ine ndidzapitanso mwanjira yomweyo. Lidalitsike Dzina la Ambuye!” Atakhala pamenepo, akudwala zithupsya, ana ake atafa, iye anali atakanthidwa ndi usiwa, ndipo abwenzi ake onse anamutembenukira iye, mamembala ake a mpingo, china chirichonse, akudzikanda yekha ndi . . . Ndipo ndi watsoka womvetsa chisoni bwanji! Palibe aliyense wa inu amene anadutsapo mu izo. Komabe, iye anagwiritsitsa ku Mawu amenewo.

287 Iye anali mphungu. Oh, mai! Simungakhoze kumangomuphimba mmaso mwake nthawi zonse. Ayi, ayi. Zonse mwakamodzi, atayima pa Mawu amenewo, chinachitika ndi chiyani? Mitambo inayambukira mmbuyo, mabingu anayamba kubangula, mphezi zinayamba kung’anima, ndipo Yobu anayang’ana mmwamba ndipo anawona masomphenyawo, anati, “Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo. Pa masiku otsiriza Iye adzayima pa dziko lapansi ili. Ndipo ngakhale mphutsi zapakhungu zawononga thupi ili, mafupa ndi zonse, Mphamvu yofulumizitsa imeneyo idzakhala ilipo. Ine ndidzamuwona Mulungu ndekha, Amene ine ndidzamuwona ndekha. Maso anga adzawona ndipo osati wina.” Nkulondola uko? “Ngakhale impsyo zanga zikadzatha mkati mwanga, ngakhale mphutsi za khungu zimene ziri mu thupi langa tsopano, zidzawononga izo.”

288 Inu mukudziwa, mphutsi zapakhungu sizibwera kwa inu. Mphutsi imeneyo ili kale mwa inu, mphutsi zapakhungu lanu.

Kodi inu munayamba mwazindikirapo zimenezo? Atakuyikani inu mu bokosi, ndi kuliyika ilo mopanda mpweya; tizirombo tidzakudyani inu, chimodzimodzi basi, chifukwa ito tiri mwa inu. Inu mwangokhala mulu wa tizirombo, kuyamba ndi kuyamba, mkatimo.

289 "Ngakhale mphutsi zapakhungu, mphutsi zapakhungu langa zitandiwononga ine, thupi langa, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu."

290 Ndipo pa mmawa wa chiwukitsiro umenewo! Ulemelero! Aleluya! Mateyu, wolemba wamkulu uyu, 27:51, anati, "Iye atawukitsidwa kwa akufa, oyera a Chipangano Chakale, ambiri a iwo amene anagona mu fumbi lapansi, anatuluka mmanda, ndipo analowa mu mzinda ndipo anawonekera kwa ambiri." Imeneyo Mphamvu yofulumizitsa ija, inali ikanali pa mafupa a Eliya amenewo pamene panalibenso mafupa, inali ikanali pa Yobu pamene panalibe fumbi lodzaza supuni la thupi lake. Koma Mphamvu yofulumizitsa inali ikanali pamenepo.

291 "Ngati Mzimu uwu umene unamuwukitsa Yesu kwa akufa ukhala mwa inu, Iye adzafulumizitsanso thupi lanu lachivundi." Zindikirani, mwamsanga tsopano.

292 Inu mukuti, "Oh, ndikanakonda ndikanakhala moyo mmbuyo. . ." Inu mukukhala moyo mu nthawi yabwinoko. Tsopano ngati inu nonse. . .

293 Ine ndikukuwonani inu mukulemba Malemba ena. Chabwino, mulembe Atesalonika Woyamba 4:16. Zindikirani kukongola kwake, mwaona. Mu. . ."Oyera, iwo amene agona mwa Khristu, Mulungu adzawabweretsa limodzi ndi Iye," mwaona, oyera ali mmanda, akupumula. Monga Eliya anali; ena monga Elisha anali; mwaona, ena a iwo adzafulumizitsidwa, ena adzatengedwa, ena adzakhala ali mmanda. Iwo adzapita ndi Iye. "Lipenga la Mulungu lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzawuka poyamba. Ndipo ife amene tiri moyofe ndipo tatsalira tidzatengedwera mmwamba limodzi ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga." Mphamvu yofulumizitsa pa amoyo; Mphamvu yofulumizitsa pa akufa. Mukuona?

294 Mphamvu yofulumizitsa yomweyo ya Mulungu yoperekedwa mwa aneneri awiri onse awa. Tayang'anani pa maina awo, pafupifupi ofanana, Elisha, Eliya. Mukuona Mkwatibwi ndi Mkwati? Mmodzi wa iwo ndi Bambo Yesu; winayo ndi Akazi a Yesu. Inu mwaona, pafupifupi mofanana, basi—pakati pa—Mwamunayo ndi Mkaziyo. Mukuona?

295 Eliya, ndipo taonani momwe izo zikuyimiridwa apa. Tsopano, Elisha. . .Anatengedwera mmwamba mu mkwatulo, akuyimira Mpingo, chabwino, Eliya; ndipo Elisha anapuma kufikira chiwukitsiro. Mukuona? Ziri ngati mbalame, imafunika mapiko awiri kuti idzilinganize yokha. Mukuona? Mpingo unayimiridwa pomwe apo mwa aneneri awiri amenewo.

"Pakuti ife amene tiri amoyofe ndipo tatsalira mpaka kudza kwa Ambuye, sitidzawatchingira iwo amene akugona; pakuti Lipenga la Mulungu lidzalira," mapiko awiri onse adzabwera pamodzi, ndipo tidzawulukira kutali, aleluya, tidzawulukira kutali. Chifukwa, (chiyani?) mwa amoyo, kapena akufa, Mphamvu yofulumizitsayo ikadali yamoyo.

296 Zindikirani. Kumbukirani, kumbukirani tsopano, kufulumizitsidwa kudzawona chimene zinthu izi ziri. Penyani Mphamvu yofulumizitsa ya tsiku lino. Kumbukirani, ife tafulumizitsidwa. Osati kale kwambiri, ku thandizo . . .

297 Ndipo ine—ine ndikuganiza Ambuye wathu ananena, ndipo chomwechonso Paulo, "Chimene Atate anandiwonetsa, sindinabise chirichonse. Ine ndikukuwuzani inu." Ndipo mmasiku otsiriza ano pamene tinawona Mphamvu Yake yofulumizitsa pa ife, Iye mpaka anapereka Mphamvu yofulumizitsa kwa ife, kuti tiwawone odwala akuchiritsidwa. Ife tayiwona Mphamvu Yofulumizitsa ikugwira ntchito pakati pathu, monga momwe Iyo inali kumeneko mmasiku oyambirira, mwaona, kuwona Iyo ikubwerera mwa masomphenya ndi kuwukitsa akufa, kuwona Iyo ikuchiritsa odwala.

298 Tsiku lina ine ndinkamuwuza winawake, Donavon Weerts wamng'ono kuno, ine ndikuganiza inu nonse mukumudziwa iye. Ine ndinali uko ndikusaka ndi iye. Munthu wamng'ono wosauka . . . Iye ndi mnyamata wamng'ono wabwino. Iye amabwera kuno ku tchalitchi. Iye adzatero . . . Basi mzanga wabwino kwambiri. Ndipo iye basi . . . Iye anati, "Sindinafune kukuvutitsani inu."

299 Ine ndinayang'ana, ndipo khutu lake, linatembenukira njira yonse, mkati kunja. Ndipo ine ndinati, "Uli bwanji Donavon?" Basi ndinangomugwira iye pa dzanja, monga *choncho*, ndipo khansa. Ine ndinati, "Donavon, vuto ndi chiyani ndi khutu lako?"

300 Iye anati, "Sindikudziwa, M'bale Branham. Pafupifupi miyezi sikisi, seveni, ndipo ilo likungopitirira kuma . . . "

Ine ndinati, "Chifukwa chiyani sunanene kanthu za izo?"

301 Anati, "Ine—ine sindimafuna kuti ndikuvutitseni inu, M'bale Branham."

Ine ndinati, "Kodi iwe ukudziwa chimene icho chiri?"

Anati, "Ndiri ndi lingaliro."

302 Ine ndinangoyika dzanja langa pa iye, sindinanene kalikonse. Masiku awiri pambuyo pake, panalibe ngakhale chipsyera. Ndi chiyani chimenecho? Mphamvu yofulumizitsa, mwaona, Iyo idzafulumizitsa thupi lanu lachivundi. Khutu lake likanadyeka, ubongo wake ukanakhala utapita, mwaona, iye akanafa. Koma, Mphamvu yofulumizitsa! Mukuona?

303 Ndipo tsiku lina pamene ine ndinali nditatopa, inemwini, pafupifupi...Ine ndinati, "Ngati inu...Mnyamata, kulibwino upitirire, ndiwe wa usinkhu wa zaka fifite. Iwe, ngati iwe uti uchite chirichonse kwa Ambuye, iwe kulibwino ufulumire ndi kuchichita icho. Iwe ukukalamba." Mukuona? Ndipo pamenepo mmawa umenewo, Mphamvu yofulumizitsayo inabwera, ndipo Iye anandilola ine kuyang'ana kudutsa katani, ndipo ine ndinakuonani inu nonse kumeneko. Uh-huh. Mukuona? Iye anati, "Onse amene iwe unawakonda, ndi onse amene anakukonda, iwo aperekedwa kwa iwe." Mukuona? Ine ndinawawona iwo paliponse kumeneko monga choncho. Chinali chiyani chimenecho? Mphamvu Yofulumizitsa.

304 Yohane mvumbulutsi anadzazidwa ndi Mphamvu yofulumizitsa, amene anaimirira ndipo anawona mapeto kuchokera kuchiyambi.

305 Yesaya anali wodzazidwa ndi Mphamvu yofulumizitsa, ndipo anayimirira ndipo anawona Zakachikwi ndi zonse.

306 Mphamvu Yofulumizitsa! "Ndipo ngati Mzimu umene unawukitsa Khristu kwa akufa, ukhala mwa inu, Iwo udzafulumizitsa thupi lanu lakufa...thupi lachivundi." Kumbukirani, Mphamvu yofulumizitsa!

307 Taonani zimene taziwona mu tsiku lino. Mphamvu yofulumizitsa yabwera kwa ife, kuti idzatsegule Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri. Kodi chimenecho chinali chiyani, luntha la munthu? Ayi, Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu. Mwaona, Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu inaneneratu kuti izi zikanadzachitika. Mwaona, Mphamvu yofulumizitsa ya Mulungu inapangitsa dziko kuchitira umboni kwa Iyo, ndi Choonadi. Mngelo wa Ambuye, ine ndinakuwuzani inu, anali pamenepo, mu Lawi la Moto; Mphamvu yofulumizitsa inalola kuti dziko lichitire umboni kuti Iyo ndi Choonadi. Ndipo, mmenemo, iwo sanadziwe chimene Iyo inali; ndipo ife tinadziwa, tangoyang'anani mbali *iyi*, ndipo Iye ndi Ambuye wathu pamwamba apo, inu mwaona.

308 Iye ndi Mmodzi Amene anatsegula Zisindikizo zimenezo. Iye ndi Zisindikizo zimenezo, pakuti Mawu onse a Mulungu ndi Khristu, ndipo Khristu ndi Zisindikizo zimene zinatsegulidwa. Kodi kutsegulidwa kwa Zisindikizo ndi chiyani ndiye? Kuwulula Khristu.

309 Ndipo Angelo asanu ndi awiri omwewo, amene ankayimira Mipingo Isanu Ndi Iwiri yonse inatsirizidwa, ndipo ife sitinathe nkomwe kuyiwona Iyo. Iwo anatero, anatenga chithunzi, osati ife. Ndipo ndi Uyo apo, ataima pamenepo, Woweruza Wamkulu; akuwonetsera kuti Iye ndi Alfa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza. Ndi chizindikiritso bwanji! Mphamvu yofulumizitsa inachita zimenezo kwa ife.

310 Mphamvu yofulumizitsa inatilola ife kuwona kudza Kwake. Mphamvu yofulumizitsa inatikhwatula ife kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Mphamvu yofulumizitsa imapereka kuzindikira za mu mtima; kudziwa chimene chiri cholakwika ndi inu, ndi choti muchite; chimene inu mwachita, ndi chimene simumayenera kuchita; ndi chimene mumayenera kuchita, ndi chimene inu mudzakhale. Mphamvu yofulumizitsa, zinthu zonsezi!

311 Ambuye wathu Yesu ndi wodzaza ndi Mphamvu yofulumizitsa, Iye anali zonse za Iyo, pamodzi. Iye anali wodzaza ndi Mphamvu yofulumizitsa, Iye ananena izi, "Inu muphwasule thupi ili, ndipo Ine ndidzaliwukitsa ilo mmasiku atatu." Kukamba za chidaliro mu Mphamvu yofulumizitsa! "Phwasulani thupi ili, ndipo Ine ndi. . .kachisi uyu, ndipo Ine ndidzamudzutsa iye mmasiku atatu."

312 Bwanji, nchifukwa chiyani Iye ananena zimenezo? Iye ankadziwa kuti izo zinalembedwa za Iye, mwaona, kuti izo zinalembedwa za Iye, mwa Mawu a Mulungu amene sangakhoze kulephera. Mawu anati, "Ine sindidzalola Woyera Wanga kuti awone chivundi, ngakhalenso Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena." Ndipo Iye ankadziwa kuti Mphamvu yofulumizitsa imeneyo ikanamuwukitsa Iye, kuti sipadzakhala khungu limodzi lowonongeka.

313 Iye anati, "Inu muphwasule kachisi uyu, ndipo Ine ndidzamudzutsanso mmasiku atatu."

314 Chifukwa chiyani? Iwo unali ulosi, Mawu a Mulungu. Ndipo ulosi, ngati Iwo uli Mawu owona a Mulungu, sungalephere. Ndipo ulosi womwewo ndi Mawu a Mulungu amene anati Iye adzamuwukitsa Iye, amanena kuti ife tinawukitsidwa kale limodzi ndi Iye. Nzosadabwitsa Iye anati, "Musawope ayi." Ndipo kwalembedwa, kuti, "Mzimu umene ulipo tsopano, unali mwa Iye, tsopano mwa ife, umafulumizitsanso thupi lathu lachivundi." Usawope, mzanga, M-w-a-n-a wauka. Mwana wauka. Ayi . . .

315 Tsopano yang'anani pa chiwalitsiro. Ife tinali, aliyense, anaimiridwa pamenepo. Apo panali oyera amoyo amene anakwatulidwa, panali Eliya ataima pamenepo; ndipo pamenepo panaima Mose, oyera akufa anaimi-. . .Komanso, awiri onsewo anali ndi Mphamvu yofulumizitsa. Kaya mmodzi anafa, ndipo winayo sanafe, iwo onse ali pamenepo.

316 Zindikirani, oh, taonani zomwe ife tikuwona tsopano mmasiku otsiriza ano. Chinthu chomwecho chimene Iye analonjeza, Yohane 14:12. Tsopano taonani. . .[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndithudi.

Anthu amati, "Mumadzinenera kuti muli ndi mphamvu?" Ayi, ayi, ayi.

317 Ife tiri basi monga iwo pa Phiri la Chiwalitsiro, mwaona. Ndithudi, ife sitidzinenera mphamvu. Koma, ife, monga—monga iwo anali . . . Pa Phiri la Chiwalitsiro, iwo sankati, Mose, kumati, "Onani amene, onani amene ine ndiri," ophunzira kumati, "onani amene ine ndiri, onani amene ine ndiri." Inu mukudziwa chimene chinachitika? Zindikirani, iwo anamuwona Yesu akulemekezedwa. Ndizo zonse zomwe iwo ankafuna kuti aziwone zikuimiridwa, Yesu akulemekezedwa.

318 Ndipo chomwechonso lero, ife sitiyesera kuti tikhale munthu wamkulu winawake. Ife sitisamala zomwe anthu amanena za ife. Dzina lathu si kanthu; ndi Dzina Lake. Moyo wathu, si kanthu; ndi Moyo Wake. Ndi Mphamvu Yake, osati mphamvu yathu. Ndipo chiripo chinthu chimodzi chokha chimene ife timakonda kuchita, ndicho kumuona Iye akulemekezedwa. Ndipo izo zingakhale motani? Pamene Iye akulemekezedwa mwa ife, mwa chiwukitsiro Chake chimene chiri mwa ife. Ife tikumuwona Iye akuyimiridwa kachiwiri monga Iye analiri, lero.

319 Kodi inu mwamvetsa zimenezo? Mwaona, chokhumba chathu si kuti tilandire ulemelero. Chokhumba chathu si dzina linalake lalikulu. Chokhumba chathu si kutukula mpingo wina, kapena kupanga ochuluka mu Sande sukulu, kapena kuyesera kuti tibweretsemo, womangidwa, kumakankhidwiramo, kubweretsa phwando, kapena kubweretsa akatswiri, mabatani, kapena chinachake monga choncho. Chimenecho si chokhumba chathu. Chokhumba chathu ndi kumuwona Iye akulemekezedwa. Akulemekezedwa, (chiyani?) osati ndi kudzitukumula; koma mwa ife, miyoyo yathu, kutsimikizira kuti Iye ndi wamoyo ndipo akukhala mwa ife.

320 Ngati ine ndingadzichotsepo ndekha panjira, kuti pamene William Branham sakuganiziridwa nkomwe, ndipo inu osaganiziridwa nkomwe, mpaka ife titamuwona Yesu akulemekezedwa pakati pathu. Kumuwona Iye, ndicho chokhumba chathu. Ndiyo yofulu- . . . zimatipatsa ife Mphamvu yofulumizitsa. Ndipo izo zimatipatsa ife chimwemwe, kudziwa kuti tiri ndi Iye, ziwiri zonse mnofu ndi fupa la Iye, pokhala Mkwatibwi wa Iye; ndi kuwona njira Zake zotsimikizidwira, kutsimikizira mwa ife kuti Iye tsopano wauka kwa akufa. Mukuona?

321 Nzosadabwitsa Iye anati, "Musawope", pakali pano, zindikirani, ife tawomboledwa ndi Iye, ndipo tsopano tawuka ndi Iye. Icho ndi chimene Isitala imatanthauza kwa anthu, "tawuka ndi Iye"! Zindikirani. Tsopano ife tiri ndi Mzimu Wake mwa ife, chikalata cha mtheradi chalipiridwa kwathunthu.

322 Ayi, inu simumati, "Chabwino, ine ndikuyembekeza ine ndikwanitsa izo." Inu mwakwanitsa kale izo. Osati, "Ine *ndi*kwanitsa." Ine ndakwanitsa kale. Ine sindinakwanitsepo; Iye anandipangira ine. Mukuona? Osati ine; Iye! "Chabwino, M'bale

Branham, iwo amati . . . " Ine sindisamala zomwe iwo akunena. Apo Iye anandipangira izo, kwa ine. Ndizo zonse zimene ine ndikufuna, ine ndikusamala.

323 Ine basi—ine ndikungofuna kuti ndimuwone Iye akuwonetseredwa. Inu mungakhoze bwanji kuchita izo, kumuyitanira Iye kumeneko? Ayi. Iye ali mwa inu. Mwaona, Iye ali mwa inu. "Chabwino, ndiye, Ambuye, ngati ndingadzichotsepo ndekha panjira, Inu mukhoza kuwonetsera. Inemwini . . . Inu mungachite bwanji izo? Chifukwa Inu munazikonza izo chomwecho. 'Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera.'" Zindikirani. Ulemelero!

324 Ndi umboni wonse umenewo utasonkhanitsidwa, uli ndi ife tsopano mmawa uno, oh, ine ndikuganiza za nyimbo ija:

> Mmawa wa chiwukitsiro uja,
> Pamene zingwe za imfa zidzaduka,
> Ife tidzauka, (Aleluya!) tidzauka.

325 Inu mukukhulupirira zimenezo? Ife tidzauka! Mwa Iye ife timakhala gawo la Iye, Isitala, chinsinsi chowululidwa cha Mulungu monga chinaliri pamenepo, cha Moyo pambuyo pa imfa. Ife tiri amoyo tsopano, amene nthawi yina tinali akufa mu tchimo ndi zolakwa. Chisindikizo choona cha Isitala chaphwasula imfa pondizungulira ine, ndipo ndine wamoyo. Chisindikizo cha Isitala, pachiyambi, chinaphwasula chisindikizo cha Chisindikizo cha Chiroma, Chisindikizo cha Isitala, chimene Iye anasindikizidwa nacho. Ndipo anthu, pamene iwo anafa, anali atapita; koma Iye anamatula chisindikizo ndipo anawulula chinsinsicho. Ndipo tsopano Mulungu, mwa Mzimu Wake Woyera, wamatula chisindikizo pozungulira miyoyo yathu, ndipo Khristu akuwululidwa pamene Iye akukhala mwa ife, pakuti tsopano tafulumizitsidwa ndi Iye. Oh, tsamba ndi tsamba!

> Ife tidzauka, (Aleluya!)
> Ife tidzauka! (Ameni!)
> Mmawa wa chiwukitsiro uja,
> Pamene msinga za imfa ziduka,
> Ife tidzauka, (Aleluya!) ife tidzauka.

326 Oh, kodi sindinu okondwa! Ndine wokondwa kwambiri! Kumbuyo komwe uko, mu kanyumba kakang'ono kakale ka malasha mmawa wina, zisindikizo zinamatulidwa, ndipo ine ndinawuka ndi Iye, cholengedwa chatsopano. Mphamvu Yake yofulumizitsa; Mwana wadzuka.

327 Osati kale kwambiri, ndinawuzidwa nkhani yaing'ono ya a—nsodzi. Munthu anabwera ndipo anamulemba ganyu nsodzi wachikulire kuti amutengere iye kokaweza ku Gombe la Kumadzulo. Iwo anapita mmawa umenewo.

328 Ngati aliyense wa inu anawedzapo kumeneko kadyakolo, bwanji, inu mukudziwa chimene chimachitika, kumakhala

chifunga choipa kunja uko. Ine ndikumuwona m'bale wanga wamng'ono, Eddie Byskal, kumusi uko, mmishonare kwa Amwenye kunja uko. Ndipo ife tinawedza, tokha, uko ku magombe amenewo.

329 Chotero nsodzi uyu anali ngati nyanga yobiriwira, inu mukudziwa. Iye anapita kukawedza, ndipo iwo anakokolokera kunja. Akudikirira kuti kuche, inu mukudziwa. Ndipo iwo—ndipo iwo samakhoza kumva lipenga la chifunga, ndipo nsodzi uyu anangokondowezeka yense, anati, "Kumati, ife tikutsetselekera kunyanja! Heyi!" Anali atakondowezeka yense.

330 Iye anati, "Khala pansi, mwana. Khala pansi." Nsodzi wachikulireyo, ali chete, inu mukudziwa. Iye ankadziwa chimene iye anali kuyankhula. Anati, "Ungodikira mpaka dzuwa litatuluka, ndiye ife tikhoza kuwona pamene ife tiri."

Inu mukuti, "Kodi ine ndikuyenera kukhala wa Methodisti? Baptisti? Pentekoste?"

331 Mungodikira. Mwana akudzuka, ife tiwona pamene ife tiri. Iye ndi Mawu. Dikirani mpaka mutawona Mawu akuwonetseredwa, akuwala pa Mbewu, Mtolo woweyula, ife tiwona pamene ife tiri. Kodi mukumukonda Iye?

332 Pepani ndakusungani inu nthawi yaitali. Ndi angati a inu muti mukhale usikuuno? Oh, mungobwerereranso ndiye, madzulo uno, mwaona. Pafupifupi seveni koloko? Kodi munali ndi winawakenso? [M'bale Neville akuti, "Ayi."—Mkonzi].

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

333 Kodi alipo mmodzi pano, kapena ambiri, amene alibe Mphamvu yofulumizitsa iyi mwa inu? Mwana wawalira modutsa, ndipo inu mwakhala mu kachisi uyu, inu mwamvetsera ku matepi, ndipo komabe Mzimu sunayambe wakufulumizitsani inu kufika pakuti mukhoza kutsatira Mawu a Mulungu, kuti akazi inu ndi amuna inu muthe kumvera Mawu aliwonse amene Iye anawalemba! Oh, icho ndi chinthu chowopsya. Bwanji ngati inu mukanakhala mbewu yakufa, wopanda Moyo mwa inu? Koma pali chinachake mwa inu, chimene chimakuwuzani inu, "Ine—ine ndikufuna kuti ndiwuke, mmawa uno. Ine ndikufuna kudzuka mmalo amene ine ndirimo. Ine sindikufuna kungokhala mbewu yakufa, kusiyidwa ku dothi ndi nkhuni zongoyandama. Ine ndikufuna kuti ndiwuke."

334 Kodi mungakweze dzanja lanu, ndikuti, "Ndipempherereni ine, m'bale"? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mai, tayang'anani pa manjawo; palibe njira nkomwe yoitanira kuguwa. Chimene ife timachitcha kuyitanira kuguwa, anthu amabwera mozungulira guwa, ine sindiri mochuluka kwambiri pa izo, mulimonse. Izo zinangowonjezeredwa ku mpingo mmasiku a chitsitsimutso cha Methodisti. Mukuona?

335 Baibulo linati, “Onse amene anakhulupirira,” mwaona, “anabatizidwa.” Pali dziwe apa, ladzaza ndi madzi, likudikirira munthu aliyense amene ali wokonzeka kuti adzifere yekha.

336 Tsopano, inu mukhoza kuyikidwamo, kanthawi kangapo, mu Dzina la Ambuye Yesu; koma kufikira mbewu imeneyo itakhala Moyo, mwaona, Iwo sungafulumizitse iyo. Ayi, ayi, ayi. Ubatizo wa mmadzi uli ngati mame amene anagwa kuchokera kumwamba; iyo ikhoza kugwera pa mbewu, koma, mulibe Moyo mmenemo, iyo siyingakhale moyo.

337 Koma ngati ubatizo weniweni wa madzi umenewo, wa imfa kwa inueni, ndipo ndinu okonzeka kuti mufe ku chirichonse chimene inu munayamba mwaphunzitsidwapo ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, zomwe ziri zotsutsana ndi Mawu, ndipo inu mudzayenda ngati mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu, ndipo inu mukutanthauza izo mu mtima mwanu, muwone chimene ubatizo wa madzi umenewo uti uchite kwa inu mmawa uno. “Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha zolakwa zanu, tchimo lanu, ndipo mudzalandira Mtolo, nsembe yoweyula. Inu mudzalandira Zimphamvu, Mzimu Woyera. Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa iwo onse. Kwa timibadwo tonse, izo zidzakhala.”

338 Atate Mulungu, ine—ndayankhula motalika, ndipo ndatenga nthawi yambiri ya anthu, koma, Ambuye Mulungu, palibe poyimira kwa izo. Izo zikungowoneka kuti inu mukungoyenera kusiya ndi kuchokapo, ndi kukapuma, ndi kudzabwerera. Ife tikukhala mu dziko lakufa, pakati pa anthu akufa; ndi Uthenga wa Moyo, ndi umboni wa chiwukitsiro. Wokondedwa Mulungu, ife tidzangokhala achivundi kamodzi, ndipo kodi zidzakhala bwanji ngati tingalole mwayi uwu kuti utidutse ife?

339 Mitima yathu ikuyaka; miyoyo yathu ndi yokondowezedwa; awa amene abwera. Ndipo ambiri pano akumvetsera Uthenga uwu mmawa uno. Inde, thuu kapena firi handirede anakweza manja awo. Iwo akufuna kuti akhulupirire, Ambuye. Oh, ndithudi mbewu imeneyo siinafe, Ambuye. Iwo angakweze bwanji dzanja lawo monga choncho? Pali chinachake. O Mulungu, ndi mwiniwake wakale, ndi mkazi uja wa Yobu wayima pamenepo, akuti, “Oh!” Koma, Ambuye, mulole Yobu ameneyo, wokhulupirira ameneyo, abwere, mmawa uno, afe kwathunthu, ndipo aikidwe muno mu ubatizo wa mmadzi uwu.

340 Mame amene amabwera kuchokera Kumwamba, Mawu a Mulungu amene amati Iwo adzatsuka tchimo lirilonse ndi kulichotsapo ilo! Inu mumabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, chifukwa chiyani? Chikhululukiro cha tchimo lanu, machimo amakhululukidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

341 Mulole, ndiye, Atate, mulole. . .Ngati iwo akudwala, mulole iwo atuluke ali bwino. Mulole, ngati iwo ali olumala, mulole

iwo ayende pansi pa Mphamvu ya Mzimu Woyera. Ngati iwo akhala ali ochimwa, mulole iwo atuluke atatsukidwa ndi oyera. Ndipo zimango, polowa mkati; Zimphamvu zibwere kuchokera Kumwamba, Mzimu Woyera, ndi kudzawatengera iwo kutali, Ambuye. Fulumizitsani thupi lawo lachivundi, ndiye ife tidzamva malirime enieni atsopano, mphamvu za Mulungu, chikondi chosaneneka, chisomo chakufa ndi chisomo chamoyo; ndi Khristu wowukitsidwa, Thupi, Mkwatibwi womuyimira Iye pa dziko lapansi.

342 Atate, iwo ndi Anu. Iwo anakweza manja awo. Ine ndalalikira Mawu. Tsopano, Atate, alandireni iwo, ine ndikupemphera. Mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikupempha izi. Ameni.

343 Inu mumamkonda Iye? Kodi Iye si wodabwitsa? Kodi inu mwakhutitsidwa kuti ndinu gawo la chiwukitsiro cha Isitala icho, kuti inu munauka limodzi ndi Iye? Kwezani dzanja lanu. Inu mwaphatikizidwamo.

344 "Ana anga aang'ono," monga Paulo akananenera. Osati kuyesera kuti ndimutsanzire iye, koma, chikondi, ine ndimakukondani inu. Ine ndimadusa misewu ndi china chirichonse, kuti ndidzafike kuno, kuti ndidzayankhule nanu. Kutuluka kuchokera mchipululu, kudutsa mathithi a chipale chofewa, ndi zina zotero, kuti ndidzafike kuno. Ife timawuluka mu ndege. Inu mumayendetsa kuzungulira dzikoli, kuti tidzasonkhane pamodzi. Ife timakondana wina ndi mzake.

345 Ndife gawo la wina ndi mzake. Musadzamulole konse Satana adzakuwuzeni inu china chirichonse. Pokhala gawo la wina ndi mzake, ndife gawo la Iye. Ndipo ndife mzika zimzake za Ufumu, tikusangalala ndi madalitso awa, limodzi, a chiwukitsiro.

346 Ndipo tsopano, mwaona, tsopano inu mwawukitsidwa kale. Pamene Mulungu anamuwukitsa Iye, Iye anakuwukitsani inu. Mwanayo basi tsopano ali pa inu, ndipo tsopano inu mukukula kukhala moyo wa duwa monga Iye anali, kuti mudzawukitsidwe kwathunthu mu tsiku lotsiriza limenelo. Kuthekera kwanu, muli nako tsopano. Inu mukudziwa bwanji? Moyo wanu wasintha, sichoncho izo? Thupi lanu linabwera mu kumvera kwa Iwo, sichoncho izo? Mu kumvera kwa (chiyani, mpingo?) Mawu, amene ali Moyo, ndiye inu mwawukitsidwa tsopano kwa akufa. Ndi Isitala, ndi Yesu ndi ine. Ndi Isitara, ndi inu ndi Yesu. Ndipo ndi Isitala, ndi inu, ine, ndi Yesu. Ndife tonse. . . Kapena, Yesu, inu, ndi ine, ife tonse taukitsidwa pamodzi.

347 Ndipo ife tidzauka pa tsiku lomaliza, ngakhale mizimu yathu itachoka mmatupi athu, ngakhale matupi atachita dzimbiri, mulole iwo apite ku fumbi, mulole iwo awotchedwe, mulole iwo akhale pansi pa nyanja. Baibulo linati, "Mngelo anatsanulira yake pa nyanja, ndipo chirichonse chimene chinafa chinatulukira." Palibe chimene chingatibise ife, kapena

kutilekanitsa ife, kwa Mulungu amene ife timamukonda bwino kwambiri, amene anatiukitsa ife palimodzi.

348 Mulungu akudalitseni inu. Ine ndakusungani inu pano nthawi yaitali. Ngati anthu amenewo akadali pa lamya imeneyo, iwo ndithudi. . .Pa masenti fifite pa miniti, iwo alipiradi kwenikweni, mmawa uno. Koma, ine sindikanatha kuyima pa ora limenelo, ndimangoyenera kupitiriza.

349 Tsopano, Ambuye akalola, ine ndibwerera usikuuno, kuti ndidzayankhulenso nanu kachiwiri. Ndipo ngati sindingathe, ndipo kenako nonse mukudziwa . . . Ndikuganiza kuti ife sitiri pa ayi . . . kapena ayi . . . Kodi sitilinso pa foni? Sitilinso pa foni.

350 Inu nonse mukudziwa kumene ine ndikupita, sichoncho inu? Afrika! Ine ndaitana kwa nthawi yaitali; kwa zaka ndayesetsa kuti ndibwerere. Tsopano masomphenya, Mzimu wa Ambuye wakonza njira. Iwo anati, pamene mbadwa zosauka zija zinamva izo, kuti ine sindinabwere nthawi yotsiriza pamene ine ndinali kumeneko, iwo anagona pansi usana ndi usiku, ndipo anabuula ndi kulira, ndi kumati, “Ambuye, ife tachita chiyani?” masauzande a iwo. Anthu amenewo samakhulupirira nkomwe kuti ali ndi solo. Mukuona? Ndipo iwo analira ndi kubuula, ndipo iwo analira.

351 Musatumize mawu patsogolo. Chonde musatero. Mwaona, ngati visa ingapezeke kuti yadutsa kumeneko ndi kukafika pakati pa atumiki amenewo, iwo angandiletse ine apo pomwe. Ine ndiyenera kupitako ngati wosaka. Ine ndikupita kwa mfumukazi amene anabweretsa sitima seventini zodzadza uko ndi kubwera ku msonkhano. Ndikuyenera kupita kukasaka mu dera lake. Ndipo ndidzapitako, pasipoti yanga ndi chirichonse zikutchula za wosaka, osati msonkhano wachipembedzo.

352 Ndiye padzakhala m’bale mmodzi adzakomana nane, adzati, “Bwanji osangokhala ndi msonkhano waung’ono wa ife?” Mabwalo ampira abwerekedwa kale. Iwo sakudziwa nkomwe zimenezo. Mukuona? Oh, ulemelero!

353 Mupemphere kuti chifuniro cha Mulungu chisalepheretsedwe. Kuti, solo yanga imene yalirira Afrika kuyambira pamene ine ndinachokako, mulole kuti ine ndidzathe kubwerera kachiwiri, kenako nkudzakubweretserani inu uthenga wa msonkhano wopambana. Ine mwinamwake sindidzakuwonaninso inu, kuyambira lero, mpaka ine ndidzabwerere. Ife tikupita, mmasiku ochepa okha tsopano, pa teni Meyi. Kodi inu mundipempherera ine?

354 Kumbukirani, inu simukudziwa chimene mavuto ali, mpaka inu mutafika pamenepo; asing’anga mbali zonse zonse, ndi mdierekezi, ndipo musaganize kuti iwo samadziwa choti achite. Mukuona? Ndipo iwe umayenera kudziwa zomwe ukunena, pamene iwe wayima pamaso pawo. “Koma ine ndikumudziwa Yemwe ndamukhulupirira, ndipo ndine wokakamizika kuti Iye

ndi wothekera kuti asunge chimene ine ndachipereka kwa Iye kufikira tsiku limenelo."

Tsopano, pali mipango ina ili apa.

355 Wokondedwa Mulungu, monga Uthenga uwu mmawa uno, wa chiwukitsiro, ndipo ine ndaima pano, Ambuye, ndi kutsimikizira mwa Mawu kuti Mphamvu yofulumizitsa iyo ili mwa mwana wokhulupirira. Chotero, pa kukhulupirira, mu chikhulupiriro, kuti Mphamvu yofulumizitsa iyo yasintha moyo wanga. Ndipo anthu awa akukhulupirira, Ambuye, ndipo Iyo yasintha miyoyo yawo. Ndipo ife tikupempherera wina ndi mzake.

356 Ine ndikuyika manja anga pa mipango iyi, kuti... Mulole Mulungu, Amene anamufulumizitsa Yesu Khristu ndi kumutulutsa Iye kwa akufa, ndipo Mzimu umenewo umene unamuwukitsa Iye kwa akufa, ukhale mu thupi lathu.

357 Mzimu umene unali pa thupi la Elisha, umene, atafa ndipo popanda kanthu koma mafupa, iwo anali ndi Mphamvu yofulumizitsa mwa iwo. Manja a atumwi anali ndi Mphamvu yofulumizitsa mmenemo. Malingaliro a atumwi, kuwona kwa atumwi, a—malirime a okhulupirira, onsewo anali ndi Mphamvu yofulumizitsa.

358 Tsopano mulole Mphamvu yofulumizitsa imeneyo, pamene ine ndikuyika Mawu awa pa iwo, ndi manja anga kuti amuimirire mwiniwakeyo, mwa chisomo, cha Mphamvu yofulumizitsa imeneyo, mulole Iyo ifulumizitse lirilonse la matupi odwala awa, ndipo iwo akhale athunthu kachiwiri, Mulungu, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu.

359 Mulole izo osati kwa mipango iyi yokha, koma kwa anthu awo kunja uko mwa omvetsera, aliyense amene akuvutika. Ana aang'ono amenewo, anthu okalamba, chirichonse chimene iwo ali, mulole Mphamvu yofulumizitsa imeneyo iwafulumizitse iwo pakali pano, mu Dzina la Yesu. Ameni.

360 Tsopano, ndi angati ali ndi Mphamvu yofulumizitsa? Tsopano ikanani manja pa wina ndi mzake, ngati Mphamvu yofulumizitsayo ili mwa inu.

361 Tsopano, pali chinthu chimodzi chokha choti mupewe kuti Iyo, isasokonezeke, ndicho kusakhulupirira kwanu. Mkazi anakhudza chovala Chake, anachiritsidwa; msirikali Wachiroma analavulira pa nkhope Yake, ndipo anapita ku gehena. Mukuona? Chotero izo zimatengera...zimatengera pamene iwe uli. Kodi inu mukuikhulupirira Iyo? Kodi inu mukuikhulupirira Iyo?

362 Tsopano ine ndikufuna inu muweramitse mitu yanu ndi kupemphererana wina ndi mzake. Basi—basi mungopemphera pamenepo, basi muziti, "Ambuye, munthu uyu"...Mwaona, mungopempherana wina ndi mzake.

363 Wokondedwa Mulungu, ife tikuchita izi mu Dzina la Yesu Khristu, Dzina lokhalo loperekedwa pakati pa anthu limene ife tikhoza kupulumutsidwa nalo kapena kuchiritsidwa. Anthu awa, amene ali nzika zimzathu za Ufumu, eni a Mphamvu zofulumizitsa, fulumizitsani Iyo kwa iwo, Ambuye, pakali pano. Ndipo mulole Mzimu upite kuchokera kwa mphungu kupita kwa mphungu, kuchokera ku Mawu kupita ku Mawu, mpaka chidzalo cha Yesu Khristu chitawonetseredwa mu thupi lirilonse, ku zakuthupi, zauzimu, kapena chosowa chirichonse chimene iwo akuchisowa, pamene ife tikuyikana manja athu pa wina ndi mzake. Mu Dzina la Yesu Khristu.

65-0418M Uku Ndi Kutuluka Kwa Dzuwa
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org